# *Khristu Wozindikiritsidwa Wa Mibadwo Yonse*

Zikomo inu, m'bale. Mukhoza kukhala pansi. Ndithudi ndikuwutenga uwu kukhala mwayi waukulu usikuuno, kudzakhala kuno ku Louisville, Mississippi. Ife takhala tikuyembekezera nthawi iyi, kwa nthawi ndithu, ndipo ine ndinaganiza kuti ndidzafike ku Louisville. Ine ndiri kutsidya kwa mtsinje basi kuchokera ku Louisville, Kentucky, kumudzi kwathu. Zikuwoneka ngati ndikubwereranso kwathu, kudzakhala mu Louisville.

Tsopano, kumtunda uko, ena a iwo amakutcha uko "Luavul," "Louis-ville," ndi "Lueyville." Ndipo sindikudziwa kuti kuno amakutcha iko chiyani. Ine ndikuganiza kuti ife, njira yabwino, momwe ine nthawizonse ndakhala ndikutchulira iwo, ndimati Louis-ville. Zimawoneka ngati L-o-u-i-s- angakhale Louis-ville. Koma, kwathu uko ndi "Luavul," ndi "Lueyville," ndi "Louis-ville," kotero timangotenga kusankha kwathu, limene ife tikufuna kuligwiritsa ntchito.

Chinthu chofunikira ndi, chakuti, ife tasonkhana pamodzi mu Dzina la Ambuye Yesu. Ife tasonkhana pano osati pa cholinga china koma kudzamutumikira Iye, ndi kuti Dzina Lake lalikulu likhoze kulemekezedwa pakati pathu mochuluka pamene ife tiri—pamene ife tiri . . . msonkhano ukatha, kuposa momwe Ilo likanakhozera, ngati nkotheka, monga Ilo lingakhalire tsopano. Ife tikudziwa kuti timamulemekeza Iye ndi mtima wathu wonse.

Ndipo tsopano ine ndabwera kuno pa kuyitanidwa ndi atumiki a kuno, dera lozungulira kuno, ndi malo ano. Ndipo ine sindinabwere ndi chinachake chosiyana ndi iwo; Uthenga womwewo basi. Ine ndikukhulupirira, Yesu ananena nthawi ina, kuti, "Ufumu wa Kumwamba uli ngati munthu amene anatenga a—khoka ndikupita kunyanja. Ndipo pamene iye analiponyera ilo mkati, iye anakoka mitundu yonse." Tsopano, izo ndi zomwe timapeza mu ukonde wa Uthenga.

Pamene munthu aponyera ukonde mu nyanja yayikulu kapena mu nyanja, iye samadziwa nkomwe chimene iye ati achipeze kuchokera mmenemo. Chifukwa, iye akhoza kugwira nkhanu. Ndipo iye akhoza kugwira zodya nsomba. Iye akhoza kupeza akangaude, njoka, ndi—ndi chirichonsecho.

Koma, ndi ntchito yathu kuti tiziwedza. Si ntchito yathu kuti tiziweruza. Ndipo ndabwera kudzatenga ukonde wanga, umene Ambuye wandipatsa ine, ndi kudzamangiriza pamodzi ndi ukonde wa amuna awa, kuti, ife, maukonde awiri afikira

patali pang'ono basi kuposa momwe ukonde umodzi ungachitire. Kotero, ine ndamangiriza ukonde wanga ndi inu abale pano. Anthu nonsenu pano, amene muli a mipingo iyi kuzungulira kuno, ndamangiriza ukonde wanga ndi inu, kuti ndiwuponyere mu nyanja muno, ndi kukokera mkati ndikuti ndiwone ngati Ambuye ali ndi zina—zina mkati muno zimene sizinagwidwebe. Ndipo mulole Uthenga wopambana wa Ambuye wathu Yesu Khristu uzindikiritsidwe kwambiri pakati pathu, mmausiku faivi otsatirawa pano, kuti ife tiwone onse amene sanagwidwe, pa m'badwo uno, kuti akhoze kugwidwa mu—ukonde wa Uthenga, kuti agwiritsidwe ntchito ndi Mbuye.

Tsopano, ife, izi sizingakhoze kuchitidwa pazokha. Izo zikuyenera kuchitidwa ndi mgwirizano ndi pemphero, ndi tonse pamodzi, kugwirizana pamodzi ndi kudzayika mitima yathu pamodzi, ndi kupemphera.

Ndipo tsopano ife tasangalala ndi chitsitsimutso cha pafupifupi zaka fifitini, chimene malingana ndi mbiriyakale ndi chotalika kuposa chitsitsimutso chirichonse chimene chinayamba chakhalapo, mwa kudziwa kwanga. Kawirikawiri, chitsitsimutso chimatenga pafupifupi zaka zitatu, kenako icho chimabalalika. Koma pokhulupirira kuti ichi ndi chimodzi mwa zitsitsimutso zazikulu zomaliza zomwe dziko lapansi lidzalandire, ndipo chabwera mu m'badwo wotsiriza, m'badwo wa Laodikaya, pa mapeto pa nyengo ya Chipentekoste. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti mpingo tsopano ukupita mu kufunda kwake, monga Baibulo linaneneratu. Ndipo ife tikungowona basi kuwedza kwa gawo lomaliza, pamene ife tikuziwona zinthu zikuchitika monga zakhala zikuchitikira mdziko, m'masiku angapo apitawa.

Mwachitsanzo, chivomezi chachikulu ku Alaska. Sipanayambe pakhalapo chivomezi ngati chimenecho, mdziko lonse. Kodi inu munazindikira? Icho chinabwera pa Lachisanu la Paskha. Inu mukudziwa, nthawi yotsiriza imene dziko linagwedezekapo inali pa Lachisanu la Paskha, aponso, pamene Mbuye wathu anafa, ndipo icho chinagwedeza dziko lonse lapansi. Ndipo kumbukirani, icho chikhoza kukhala chizindikiro cha kubwereranso kwa Iye. Iye ananena kuti kudzakhala zivomezi m'malo osiyanasiyana. Lero tinali nacho china ku California, ndipo izo zikungowonekera kulikonseko, zivomezi zopepuka. Ife tikuzindikira, ngakhale Nyumba yayikulu yachoka pamalo pake, ndipo yabwerera m'mbuyo. Ndipo—ndipo kumusi kuno ku Baton Rouge, Louisiana, kuli dziwe losambiramo uko, chinamwazira madziwo kunja, kuchokera ku Alaska. Uko ku Switzerland, Sweden, ndi kudutsa uko, chinagwedeza nyumba ndi zinthu, kuzungulira dziko.

Ine ndikukhulupirira kuti izo zikuyesetsa kuti zitsegule maso athu, kuti tiwone ora limene ife tikukhalamo. Ine ndiri pano mu mantha aumulungu, kuti, izo zikhoza kukhala

mofulumira kuposa momwe ife tikuganizira, za kuwonekera Kwake.

Ndipo m'bale ndi mlongo, ngakhale kwa ana aang'ono, tiyeni tiyike kuwonamtima konse kumene tingathe. Ichi chikhoza kukhala chitsitsimutso chotsiriza chimene ife tikanati tidzakhaleko, ndipo ife mwinamwake sitingathe kuchimaliza ichi, kufikira Kudza Kwake. Ine ndikumuyembekezera Iye lero. Ngati Iye sabwera kuno lero, ine ndidzakhala ndikumuyembekezera Iye mawa, ngati ine ndiri kuno. Ndipo ine ndakhala ndikumuyembekezera Iye tsopano, kuyambira pamene ine ndinamva za kubwereranso kwa Iye, ndipo izo zakhala ziri zaka sarte-firii zapitazo pamene ine ndinapereka mtima wanga kwa Iye. Ine ndakhala ndiri kuseri kwa guwa, kwa zaka sarte-firii, kuyesetsa ndi kulengeza chuma Chake chosafufuzidwa cha ulemelero Wake. Ndipo ine ndikudalira kuti Mulungu adzizindikiritsa Yekha chomwecho pakati pathu, mpaka kuti wosakhulupirira aliyense apulumutsidwa, ndipo odwala onse achiritsidwa, ndi oyera a Ambuye, Ana ake okhulupirira, adzakwezedwa m'mwamba—mu Mzimu.

Chitsitsimutso sichimatanthauza kupeza mamembala atsopano. Ndi kutsitsimutsa icho chimene ife tiri nacho kale. Mukuona? Ndi kutsitsimutsa.

Ine ndinayima, nthawi ina kalelo, ndipo ndinkawona mafunde pa Nyanja ya Michigan, kumawona, nditayima kunja uko, chitatha chitsitsimutso chachikulu ku Chicago. Ine ndinawona—mafundewo, momwe iwo ankabwerera, mu mafunde aakulu basi, akusesera mkati ndi kunja. Ine ndinaganiza, inu mukudziwa, zinandikumbutsa ine za nyimbo, "Kusefukira kwa chimwemwe pa moyo wanga, monga mafunde a nyanja akugudubuzika." Ndipo mafunde amenewo amayambira kwinakwake, uko mu nyanja kapena mu nyanja yayikulu. Ndipo pamene iwo akubwera, iwo amatenga mphamvu, nthawi zonse. Ndiye, potsiriza, iwo amadzamenya pa gombe; kudzangotuluka, kuti adzalowenso kachiwiri.

Ndipo umo ndi momwe mafunde a ulemelero wa Mulungu amachitira. Iwo amabwera mkati, basi monga—basi monga kugudubuzika, mobwereza ndi mobwereza, mmbuyo ndi mmbuyo, ndi mmbuyo ndi mtsogolo, mafunde a chimwemwe cha Mulungu amagudubuzika mmiyoyo yathu.

Ine ndinadabwa, "Kodi cholinga cha zimenezo chinali chiyani? Kodi cholinga chogwedezera madzi mmwamba-ndi-pansi ndi chiyani?" Chirengedwe chiri nayo njira yodzisamalira chokha.

Monga ngati anthu, tsopano, pamene inu muli mu mpingo wanu ndi abusa anu, pamene mukukhala ndi phunziro la Sande sukulu kapena—kapena chinachake mu mpingo wanu. Mwinamwake mulibe chisangalalo chikuchitika, kapena—

kapena mulibe chachilendo. Koma, komabe, mumangokhala Mulungu wochuluka mu mtima mwanu monga momwe amakhalira pamene inu mukudumpha mmwamba-ndi-pansi kapena kufuula.

Ine ndinaganiza, "Iwo amachita izo chifukwa chiyani?" Cholinga chomwecho chimene Mulungu ali nacho, chitsitsimutso, ndi cholinga chomwecho chimene Iye amayikira chitsitsimutso pa nyanja yayikulu, kuyika chitsitsimutso mu nyanja. Ndipo madziwo, akamagwedezeka mmwamba-ndi-pansi, amachotsa zinyalala zonse mmadzimo, amakaziponyera izo pa gombe. Ndipo ine ndikuganiza kuti icho ndi chinthu chabwino, kuti ife tizikhala ndi zitsitsimutso, ndi kukhala ngati kuchotsa zamatsenga zonse kwa ife, ndi zonse—a—dziko kunja, kuligwedezera ilo kunja, ndi kuliponyera ilo pa gombe, kotero kuti madziwo azikhoza kukhala opanda zoterozo.

Tsopano, usikuuno, izo ziri ngati . . . Nthawi yoyamba imene ine ndinayamba ndakhalapo kuno, ndipo komabe ine sindikumverera ngati ndine mlendo pakati panu. Ine—ine sindiri. Ine ndine m'bale wanu. Ndipo ine—ndipo ine, ndithudi, chitsopano chongodziwana wina ndi mzake . . . Mwinamwake, ena a inu, ndikudziwa kuti sindinakuwonenipo. Mwinamwake inu simunandiwonepo ine. Ndipo nthawizonse pamakhala kumverera komangika pang'ono kumeneko kumene inu mumangokhala . . . Izo ndizovuta. Ndipo ife basi . . . Izo zimangokhala mwanjira imeneyo, tsopano, konsekonse. Ine ndikupanga, ndikuyamba ulendo wanga wachi eyiti kuzungulira dziko lapansi. Ndipo ine—ine—ine ndimazipeza izo, konsekonse, ziribe kanthu kumene iwe uli.

Koma pamene iwe uwapeza anthu Achikhristu, kumene kuli Mzimu Woyera, ziribe kanthu ndi fuko liti, kaya ndi kutali bwanji mu nkhalango, kapena chirichonse chimene icho chiri, iwo amachita chinthu chomwecho chimene inu mumachita pamene inu mwalandira Mzimu Woyera. Iwo amachita chinthu chomwecho basi. Iwo amakhala ndi ufulu womwewo, umene iwo ali nawo. Iwo amakhulupirira mwanjira yomweyo ndipo amachita mwanjira yomweyo mmene Mkhristu aliyense amachitira akamulandira Khristu.

Koma, mmenemo, inu mumapeza kumangika kumeneko. Ndipo, ine ndikuganiza, usiku woyamba ndi nthawi yabwino yoti tingokhala ngati tizolowerane. Ndiyeno, tsopano, ndiye, pamene msonkhano uzikhala ukupitirira ndi kumapitirira, ndiye tidziwana kwambiri wina ndi mzake kuposa momwe tiriri tsopano. Koma, mwamsanga ife tikamadzatulukamo, bwanji, ife tidzakhala abwinoko.

Mzimu Woyera ndi wamanyazi, kwambiri, wamanyazi kwambiri. Ndipo—ndipo pamene inu muli ndi wosakhulupirira mmodzi yekha kapena wokayikira atakhala pamenepo, Mzimu

Woyera sungathe kugwira ntchito basi, nkomwe. Kumbukirani, Yesu anamutsogolera munthu kumutulutsa mu mzinda, kuti akamuchiritse iye, nthawi yina, anamuchotsa iye ku kusakhulupirira. Iye anabwera mu mzinda Wake Womwe, ndipo Baibulo linati, "Ndipo ntchito zamphamvu zambiri Iye sanathe kuzichita." Ife sitikufuna kuziganizira izo mwanjira imeneyo, koma Baibulo linati Iye sakanakhoza kuchita izo. Mukuona? Iye sangachite chirichonse popanda chikhulupiriro chanu. Inu mukuyenera kukhulupirira zimenezo.

Winawake anandiwuzapo ine, nthawi zambiri, kuti, "M'bale Branham, ine sindikusamala chimene chingachitike; Ine sindimakhulupirira Izo." Chabwino, Izo sizinali kwa munthu ameneyo.

Izo si za osakhulupirira. Ndi za okhulupirira okha, iwo amene akukhulupirira. "Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira." Osakhulupirira samapeza kalikonse. Ndipo kotero iwo—iwo samakhulupirira kalikonse, kotero kuti sapeza kalikonse. Ngati iwo angokhala ndi zafioloje zozizira, izo ndi zomwe iwo amapeza. Koma iwo amene amakhulupirira mwa Mulungu, ndi kukhulupirira kuti Yesu Khristu ali weniweni lero basi monga Iye anali nthawizonse, izo ndi zomwe iwo amalandira. "Basi molingana ndi chikhulupiriro chanu, izo zikhale kwa inu."

Ndiyeno mkati muno, ine ndimaganiza kuti ndipereke, usikuuno, chimene ife tikuyesetsa kuti tichite.

Tsopano, ine ndikupenekera, pokhala kuti uwu ndi othandizidwa ndi Achipentekoste, kuti ambiri muno ndi anthu Achipentekoste. Ndipo apo ndi pamene ine ndinaponyera mayere anga, ngakhale ine sindinajowinepo konse mpingo wa Chipentekoste uliwonse, ndipo palibe mpingo winawake. Ine ndiribe chipembedzo chirichonse, chipembedzo chinachake. Ndipo, moona, sindine mochuluka kwambiri wa zimenezo. Iwo akhoza kukhala nacho chirichonse chimene iwo akuchifuna. Koma inu mumalemba mizere, inu mukuona, ndipo Mulungu—Mulungu samakonda kuti mizere izilembedwa mu Mpingo Wake.

Zikundikumbutsa ine za munthu, nthawi yina, anali ndi abakha ena, ndipo iye—iye anadula mapiko awo kotero kuti iwo asamathe kuwuluka kuchoka mu khola. Iye anali ndi abakha ena mbali imodzi, ndi abakha mbali inayo. Madzi anayamba kubwera mkati. Chinthu choyambirira inu mukudziwa, madzi anayamba kukwera ndi kukwera, ndipo abakhawo anasonkhana pamodzi pamenepo. Mukuona? Icho ndi chimene ife tikuyenera kuchita. Mulole madziwo ayambe kukwera, ndipo zikatero abakhawo azisonkhana pamodzi, inu mukuona, pamenepo. Ndipo ife tonse tiri m'madzi omwewo. Kotero, zotchinga

zachipembedzo zikhoza kuyandamitsidwira kunja, ngati ife titangowalola madziwo kuti alowe okwanira.

Monga munthu anali ndi munda wa chimanga. Wina anapitiriza kumanena...Iye anali nazo mmunda umodzi, zomera za mbali *iyi*; zinazo mbali *iyi*. Ndipo kotero wina akuwulukira apo, mmawa uliwonse, amakhoza kumayang'ana pa munda wa chimanga umenewo. Iye anati, "Kodi uwo si munda wa chimanga wabwino *apa*, ndipo wina *apo*!" Chimangacho chitatalika pang'ono, chitafika njira yonse kupitirira mpanda, unkawoneka ngati munda umodzi. Kotero ine ndikuyembekeza kuti izo zikhala mwanjira imeneyo pano, kuti ndife wawukulu umodzi, munda wawukulu wa chimanga wamtima-ndi-mtima wa Ufumu wa Mulungu.

Tsopano, cholinga chathu.

Tsopano, nthawi zambiri, anthu amati, "M'bale Branham, mchiritsi Wauzimu." Ayi. Zimenezo ndi zolakwika. Alipo mchiritsi mmodzi yekha; ameneyo ndi Mulungu. Palibe mankhwala amene ali ochiritsa, palibe dokotala amene ali wochiritsa. Palibe dokotala wabwino amene amadzinenera kuti ndi mchiritsi. Ndipo ngati iye amatero, ndiye iye—iye—iye akukuuzani inu chinachake cholakwika.

Ine ndinafunsidwapo kwa Mayo Brothers, ndipo iwo anati, "Ife sitimadzinenera kuti timachiritsa odwala, Bambo Branham. Ife timangonena kuti timathandizira chirengedwe. Alipo mchiritsi mmodzi; ameneyo ndi Mulungu." Ndipo zimenezo ndi zanzeru bwanji!

Inu mukhoza kuthyoka nkono wanu; adokotala akhoza kuwukonza iwo. Koma iye sangakhoze kuwuchiza iwo, chifukwa iye alibe kanthu koti achiritsire. Iwo uyenera kumanga minyewa. Adokotala akhoza kuzula dzino kapena kudula thumbo, koma ndi ndani amene angachiritse? Mwaona, Baibulo silimalakwitsa. Baibulo ndi lolondola mu Mawu aliwonse. "Ine ndi Ambuye Amene ndimachiritsa matenda anu onse." Onse! Palibe otsala! Ayi ndithu. Iwo sanapeze panobe chinthu chimene chingamange minyewa. Iwo amapeza mankhwala amene amatha kupha majeremusi, mpaka—mpaka minyewa italukana pamodzi. Koma, zimatengera Mulungu, kuti achize. Mulungu ndi mchiritsi yekhayo amene alipo.

Chotero, Baibulo ndi loona mwangwiro. Ndipo icho ndi chimene ife timayimapo: Baibulo. Izo zikuyenera kukhala PAKUTI ATERO AMBUYE. Tsopano, ife timakhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchita zinthu zimene sizinalembedwe mu Mawu Ake, chifukwa Iye ndi Mulungu. Iye amachita chirichonse chimene Iye akufuna. Ndipo, komabe, ine ndimakonda kuwona chirichonse, pamene icho chikubwera mu mzere wa chiphunzitso, chikuchokera mu Baibulo. Chifukwa, ine ndimakhulupirira kuti Baibulo ndi vumbulutso lathunthu la

Yesu Khristu. Baibulo linati icho ndi chimene Ilo liri. Ilo ndi vumbulutso la Yesu Khristu. Ndipo palibe chimene chikuyenera kuwonjezeredwa kwa Ilo, kapena chirichonse kuchotsedwa kwa Ilo. Kotero, ine ndimakonda kukhalabe mu zomwe Ilo linena ndi zomwe Ilo likulonjeza. Ngati Iye atangochita chimene Iye analonjeza, ndizo zonse zomwe ine ndimasamala kuti ndiziwone, mulimonse. Ndiye ine ndimadziwa kuti ndidzamuwona Iye.

Tsopano, mwa ichi ife sitimayesera kunena kuti ife timakhazikika mu machiritso Auzimu, chifukwa machiritso Auzimu ndi chaching'ono. Ndipo inu simungakhoze konse kukhazikika pa chaching'ono. Koma pafupifupi eyite-sikisi peresenti, ine ndikuganiza kuti zimayerekezeredwa choncho, ya utumiki wa Yesu, inali pa machiritso Auzimu. Iye. . .

Monga Dr. Bosworth ankakondera kunena, mai. . . Mmodzi wa othandizana nawo anga amene wangopita kumene ku Ulemelero, zaka zingapo zapitazi, zokhudza. . . pokhala pafupifupi usinkhu wa zaka eyite-foro. Iye anati, "Machiritso Auzimu ndi nyambo imene imakhala pa mbedza ya nsomba. Ndipo inu simumaiwonetsa nsomba mbedzayo. Inu mumaiwonetsa iyo nyambo, kotero iyo imatenga nyamboyo ndipo imakodwa ku mbedzayo." Kotero, izo, ndi zomwe izo ziri. Ife tikufuna kugwira nsomba kwa ulemelero wa Ambuye; kuzigwira izo kuzichotsa mdziko, ndi kuzibweretsa izo mu Ufumu wa Mulungu.

Ndipo chotero, machiritso Auzimu, chinthu chachikulucho ndi machiritso Auzimu a solo. Thupi la Khristu, Ilo likusowa machiritso kwambiri kuposa chirichonse chimene ine ndikuchidziwa, ndi Thupi la Khristu. Ilo lasweka kwambiri ndi zafioloje za anthu ndi kusiyana kwa zipembedzo, mpaka Ilo ndi Thupi lodwala. Ndipo ine—ndipo ine ndikukuuzani inu, Ilo—Ilo likusowa machiritso, machiritso aakulu. Kotero ine—ine ndikudalira kuti Ambuye achita chinthu chachikulu ku machiritso a gawo Lake la Thupi limene liri muno.

Ife timakhulupirira kuti ulipo umodzi, Mpingo umodzi. Ndipo ife sitimajowina konse Iwo. Lolemba likubwerali, ine ndikwanitsa zaka fifite-faivi, ndipo banja la a Branham silinandipemphe ine konse kuti ndijowine banja lawo. Ine ndinabadwa Branham. Umo ndi momwe—ndi momwe ine ndiriri.

Tsopano, umo ndi momwe ife timakhalira Akhristu. Ife timabadwa Akhristu. Ndipo inu simumajowina mmenemo. Inu mumabadwira mmenemo. Ndiye inu mumatenga khalidwe la Khristu.

Tsopano, ife tikupezanso kuti, mu izi, anthu ambiri kuno ku Amerika, makamaka, amene anaphunzitsidwa. Ife tiri ndi kachitidwe, kapena, a—Ambuye analamulira izo, kotero izo ndi zabwino, za kuyika manja pa odwala ndi kuwapempherera iwo.

Uko kunali kutuma kotsiriza kwa mpingo. Izo ndi zabwino kwambiri. Ndipo izo zakhala zikuchitidwa, kudutsa mmibadwo. Nthawi iliyonse imene chitsitsimutso chinayamba mu m'badwo uliwonse, pamakhala machiritso Auzimu ndi icho, ndi chauzimu cha Mulungu.

Ndipo tsopano ife tikupeza, mu m'badwo uno, ndi kuyesetsa kwanga, chimene ine ndikuyesetsa kuti ndichikwaniritse, ndi ichi. Pakhala pali zochuluka kwambiri mu tsiku lotsiriza lino, za anthu amene akulalikira machiritso Auzimu, ayika ulemelero waumwini wochuluka mmenemo, mpaka zapereka mawonekedwe oyipa kwa izo pamaso pa anthu. Izo zakhala ziri, "Ambuye adalitsike! M'bale *Wakuti-ndi-wakuti* anasanjika manja pa ine, ndipo, Ambuye alemekezeke, ine ndinachiritsidwa." Tsopano, ngati ine nditakhoza kuzisiya zimenezo!

Ngati wina atanena kuti, "Ambuye Yesu anandichiritsa ine," izo zingakhale zabwino bwanji, mwaona. Kotero, ndi utumiki wawung'ono umene Ambuye wandipatsa ine, ndikuyesetsa kuti ndimubweretse Iye pamaso panu, kuti inu mudzayike manja anu pa Iye, Nsembe yanu, ndi kuchiritsidwa. Si mochuluka kwambiri kuyika manjako. Chimene, ife timachita, ife tonse. Ife timapemphera ndi kuyika manja pa odwala.

Ife sitimawachiritsa anthu. Iwo anachiritsidwa kale. Munthu aliyense anachiritsidwa kale. Ndi angati akukhulupirira zimenezo? Tsopano tiyeni tiwone mmene osonkhana athu anaphunzitsidwira. Alipo magawo awiri pa atatu a iwo amene amakhulupirira zimenezo, mulimonse. Tsopano, kuti, "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa." Chikhumbo chirichonse chimene iye anachifera, pa Kalvare, ndi chathu kuyambira nthawi imeneyo mpakana mtsogolo, chirichonse chimene Iye anachifera. "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; anatundudzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa." Ife *tina*chiritsidwa, nthawi yakale.

Wochimwa aliyense ndi wopulumutsidwa. Kuyambira pa tsiku limene Yesu anafa pa mtanda, Iye anakhululukira tchimo lirilonse la munthu.

Tsopano, Mulungu ndi wamkulu—wamkulu . . . monga Munthu wamkulu. "Pachiyambi Mulungu . . . " Mukuona? Ife . . . Iye sanali Mulungu nkomwe, kuyamba ndi kuyamba. *Mulungu* ndi "chinthu chopembedzedwa." Ndipo Iye ankatchedwa . . . Panalibe chirichonse, choti chizimupembedza. Iye anali Elohim wokhalapo yekha, ndipo panalibe chirichonse choti chizimupembedza Iye. Pamene Iye analenga Angelo, ndiye panali chinachake choti chizimupembedza Iye.

Koma mwa Mulungu wamkulu uyu, Elohim, munali zokhumba. Munali zokhumba mmenemo zoti akhale Mulungu; zokhumba zoti akhale Atate; zokhumba zoti akhale Mwana; zokhumba zoti akhale Mpulumutsi; zokhumba zoti akhale mchiritsi. Zikhumbo zonsezi zinali mwa Mulungu. Ndipo ngati inu munayamba mwakhalapo ndi Moyo Wamuyaya, inu munali mu zikhumbo za Mulungu, chifukwa inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Yesu anabwera ngati Muwomboli. Ndipo *kuwombola* kumatanthauza "kuchibwezeretsa icho kumene chinayambira." Kulondola. Inu munali mmalingaliro a Mulungu. Iye akhoza kusakaniza *ichi* ndi *icho*, ndi pansi *apa* ndi pansi *apa*.

Monga munthu akamapanga maberu a tchalitchi; amayikamo mkuwa wochuluka chomwechi ndi chitsulo chochuluka chomwechi, ndipo zimaliyika ilo basi pa kalilidwe kabwino. Wowumbayo amadziwa momwe angayikiremo izo. Ngati satero, iye samapeza kaliridwe koyenera.

Ndipo Mulungu amadziwa basi ndendende kumene inu muli, ndi m'badwo umene inu mulimo. Ndipo, chotero, ngati muli ndi Moyo Wamuyaya; mawu akuti *Muyaya* ndi "chinachake chimene sichinachite kuyamba, kapena sichingathe." Chotero, aliyense amene inu munali, mwaona, inu munali, inu munali nthawizonse. Inu munali chikhumbo cha Mulungu—chikuwonetseredwa, a—Mawu. "Pachiyambi panali Mawu."

Ndipo mawu ndi ganizo lowonetseredwa. Inu mumachiganizira icho, kenako mumachiyankhula icho. Monga ndinganenere kuti, "Kuwala." Ine ndimayenera kuganiza "kuwala" ndisanati "kuwala." "Maikrofoni," ndikuyenera kunena . . . kuganiza "maikrofoni," kuti ndinene "maikrofoni."

Ndipo ndife zikhumbo za Mulungu zowonetseredwa.

Ndipo ine ndimapeza, ine ndimapeza magulu awiri a anthu pamene izo zikupitirira. Limodzi la iwo ndi achikhazikitso, ndipo linalo ndi Achipentekoste. Tsopano, Achipentekoste ali ndi chinachake, koma iwo samadziwa chimene iwo ali. Ndipo achikhazikitso amadziwa chinachake, koma alibe kalikonse ndi icho. Kotero tsopano, apo, ziri ngati munthu amene ali ndi ndalama ku banki, ndipo sangathe kulemba cheke, winayo akhoza kulemba cheke, koma alibe ndalama ku banki, ngati inu mungathe konse kuchibweretsa chinthu chimenecho pamodzi, icho chinga—chingakhale chinthu chachikulu.

Koma, tsopano, pamaso pa izi, momwe ife tikuyesetsa kuchitira msonkhanowu, ndi kufuna kuti inu, inuyo ngati munthu panokha, pa chosowa chanu mwa Khristu. Chipulumutso, machiritso Auzimu, kapena chirichonse chimene inu mukuchisowa, ndi, mwa chikhulupiriro, podziwa kuti inu muli mu Kukhalapo kwa Khristu, ndipo mwa chikhulupiriro

inu mumafikira ndi kuchipeza icho. Pakuti, ndiyo njira yokhayo imene inu muti mudzapezere izo konse. Ndi. . .Mwa chikhulupiriro ife timapulumutsidwa. Mwa chikhulupiriro ife timachiritsidwa. Mukuona? Palibe chimene Mulungu akuyenera kutsikira pansi ndi kudzachichita kachiwiri; Iye anachita kale izo.

Kotero, mwaona, chinthu chonsecho ndi—ndi, Mulungu akukhala wogwirika. Kuti, pa Tsiku lalikulu limene likubwera, pamene Khristu adzakhale pa mpando wachifumu wa Davide ndi kudzalamulira mu Zakachikwi, ndi Mulungu, wogwirika, pa dziko lapansi.

Iye tsopano ali mwa inu. Inu ndi zikhumbo Zake. Ngati inu muli ndi Moyo Wamuyaya, moyo wanu nthawizonse unalipo. Ndipo inu munali mmaganizo a Mulungu: mtundu wa tsitsi, chirichonse chimene inu muli, inu munali kuganiza kwa Mulungu, ndipo inu munangopangidwa thupi.

Ndipo icho ndi chimene Mulungu anali pamene Iye anapangidwa thupi mwa Khristu; Mulungu, akuwonetseredwa, kuwonetseredwa mu thupi, mwa Khristu. Iye anadzakhala wogwirika; Mulungu amene ife tikhoza kumukhudza. Timoteo Woyamba 3:16, "Popanda kutsutsana, chinsinsi cha umulungu ndi chachikulu: pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi." Mukuona? Mukuona? Uyo anali Mulungu akuwonetseredwa, akukonzekera.

Tsopano, ife tiri pano, mmawonekedwe awa, tikadali mophiphiritsa. Monga kutenga chithunzi cha chinachake, ndi kuchijambula icho. Mulungu anati, "Iye adzakhala ndi tsitsi lakuda, maso abuluu, ndi zina zotero. Iye adzakhala *ichi, icho*, kapena *chinacho*." Chithunzicho chinajambulidwa, usinkhu wa pafupifupi zaka twente zakubadwa, twente-thuu.

Kenako imfa imadzalowamo, iwe umayamba kufa. Ziribe kanthu ndi mochuluka bwanji momwe ungadyere, momwe ungabwezeretsere bwino chakudya m'thupi mwako, kuti chipange makungu a magazi, iwe ukufa. Ndipo mulibe wasayansi mu dziko amene angakhoze kufotokoza zimenezo.

Iwe ukamatsanulira madzi kuchokera mu chikho, kupita mu galas, iwo akatsala pang'ono kuti adzaze; ndiye ukamapitirira kutsanulira, kenako iwo amatsikira pansi. Nanga bwanji zimenezo?

Chakudya chimene umadya chimapanga makungu a magazi. Makungu a magazi amamanga thupi lako. Nthawi iliyonse ukadya, umakonzanso moyo wako katsopano. Pamene iwe unali wa usinkhu wa chaka chimodzi, nkumakula, nkumakula mpaka utafika pafupifupi twente-thuu. Ndiyeno, tsopano, inu mukudya chakudya chomwecho. Ndikumadya chakudya chomwecho chimene ndinkadya ndiri ndi zaka sikisitini. Ndiri sikisitini, nthawi iliyonse ndinkadya, izo zinkamanga minyewa

ndi kundipanga kukhala wamkulu komanso wamphamvu. Ndinafika pamapeto pa usinkhu wanga. Ndipo kenako nditamaliza usinkhu wanga, ine ndikumadya chakudya chomwecho, ndipo mwabwinoko, ndi zochuluka za izo, ndipo ine ndikukalambirabe ndi kumafookabe, nthawi zonse. Koma nthawi iliyonse ndikuwumanga mwatsopano moyo wanga, ndiye ine sindimayenera kufa. Mukuona?

Koma Mulungu anayika nthawi, ndipo munthu akuyenera kufa ndi kukayang'anizana ndi Chiweruzo. Ndipo inu mudzasunga nthawi imeneyo, abwenzi. Mungokumbukira zimenezo. Ndipo pamene ife tiri pano, usikuuno, tikufuna kuti tizikumbukira zinthu zimenezo, kuti ife tikuyenera kuti tidzasunge nthawi imeneyo. Pakhoza kukhala yambiri imene mungadzaimirire ndi kuchokapo, koma imeneyo ndi imodzi yomwe tikutsimikiza, kuti aliyense, adzakumana nayo. Ndipo tsopano, mmenemo, ndi nthawi imene Mulungu anapangana naye munthu. Thupi ili likuyenera, chifukwa lidakali chophiphiritsa. Ilo likuyenera lidzafe.

Chotero, Iye akutenga Mzimu Wamuyaya, chikhumbo Chake chiwonetseredwe mu thupi limenelo, ndiye, monga chithunzi chirichonse mu mawonekedwe ake chisanatsukidwe, icho chimapita mu chipinda chamdima. Mmenemo icho chimakatsukidwa. Chimatulukamo chiri chithunzi changwiro. Ndipo ife timapita mu chipinda cha mdima, koma timatulukamo pamene chithunzicho chakhala chiri changwiro, mu chifaniziro cha Khristu. Ife timapita m'manda a mdima, timakalowa m'chipinda chamdima kuti tikakonzedwe. Zimatengera imfa kuti ipange zimenezo.

Monga momwe zimatengera imfa, kwa inueni, kuti ipange chithunzi cha chifaniziro cha Khristu, moyo wa Khristu mwa inu. Inu mumayenera kutaya zanu zomwe kunja, kotero kuti Khristu akhoze kulowamo. Inu mumayenera kufa kwa inueni.

Momwemonso umunthu wanu umafa, kuti upangidwe ndi kuwumbidwa mu chifaniziro cha Iye. Koma pamakhalabe chikhumbo chimenecho chimene sichingawonongedwe. Icho sichingawonongedwe konse. Ndi Mulungu, pachiyambi. Ndi Mulungu pamwamba pathu, Mulungu nafe, Mulungu mwa ife. Ndipo izo zonse ndi zikhumbo za Mulungu: Moyo Wamuyaya kwa ana a anthu.

Tsopano tiyeni tipemphere.

Wokondedwa Atate Akumwamba, ife tikupemphera usikuuno kuti Inu mutidalitse ife ndi kupeza ulemelero kuchokera mu kusonkhana kwathu pamodzi. Ife tikuchipereka chipinda chino ndi mabwalowa, tikudziyika tokha pamenepo ndi kupereka izo kwa Inu, ngati chopereka, Ambuye, kwa ulemu wa Dzina Lanu. Perekani izi, Ambuye. Mudalitse chirichonse chimene ife tikuchita. Mulole icho chikhale cholemekeza Yesu

Khristu, ndi kumubweretsa Iye monga weniweni wamoyo pakati pa anthu.

2 Ndipo pamene misonkhanoyi yatha, ndipo ife tikachoka pa misonkhano iyi ndi kupita ku nyumba zathu, mulole tinene monga iwo amene zina naintini-. . .zaka zapitazo, Isitala yotsiriza iyi, pamene iwo ankachokera ku Emau, pamene Iye anawonekera pakati pawo ndipo anachita chinthu chomwecho chimene Iye anachichita asanapachikidwe. Iye anali Ambuye wowukitsidwayo, chifukwa Iye ankadzizindikiritsabe Yekha mu zinthu zomwezo zimene Iye anazichita kusanachitike kupachikidwa Kwake, ndipo maso awo anatseguka ndipo iwo anamuzindikira Iye. Mulungu, mulole ife tinene usikuuno, zitatha zaka naintini handiredi, pamene tikhale pa ulendo wathu wobwerera kwathu, usikuuno, mulole ife tinene kuti, "Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu pamene Iye anayankhula nafe panjira?" Mulole Iye adzizindikiritse Yekha usikuuno, pakati pathu, Ambuye, monga Ambuye wowukitsidwayo, atakonzeka kuti abwererenso ku Mpingo Wake. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

3 Usiku uliwonse, ndi cholinga chosunga chinthuchi mwadongosolo, ife tabwera kuti tidzapempherereredwe; M'bale Borders, kapena—kapena mwana wanga, Billy Paul, mmodzi wa iwo, azikhala pano madzulo aliwonse, pafupifupi—pafupifupi ora limodzi misonkhano isanayambe. Ndipo iwo azibweretsa makadi aang'ono amene ali ndi manambala pa iwo. Mnyamata uyu azitenga makadi awa ndipo aziwasakaniza iwo, mkati mommuno, inu mukuwona. Mukuona? Kotero, kuti, ndipo kenako azikupatsani inu khadi, lirilonse limene inu mukufuna. Pamene ine ndibwera kuno usiku, usiku uliwonse. . .Zimenezo zizimupatsa mlendo, tsiku lirilonse, a—mwayi wopeza khadi la pemphero.

4 Ndiye usiku uliwonse, si ochuluka kwambiri amene azifika pa nsanja pa nthawi imodzi, koma ine ndizibweretsa ochuluka kwambiri oti apempherereredwe. Ndikhoza kubwera, nkuyambira pa mmodzi apo, ndi foro, zikuwonetsa kuti mnyamata amene amapereka makadiwo sangakutsimikizireni inu kalikonse, kapena kugulitsa khadi la pemphero kwa inu, zimenezo zingakusonyezeni inu kuti mudzalowa mu mzere wa pemphero. Inu muli ndi mwayi womwewo, chifukwa makadiwo amasakanizidwa, pamaso pa omvetsera.

5 Chinthu china ndi, chakuti ine ndikhoza kuyambira paliponse. Ine ndikhoza kuyamba kuchokera pa fifite, kubwerera chammbuyo kuyambira pa sarte, kupita mtsogolo, kapena kuyambira. . .Ndiye nthawizina ine ndimawerenga kuti ndi angati ali mu mzere uwu, ndipo ndimawagawa iwo ndi mzere uwu, ndi zina zotero monga choncho, kuti ndipeze nambala. Ndipo nthawizina ndimatenga mwana wamng'ono, ndi kuweruza za usinkhu wake, kapena mwamuna wina

kapena mkazi, kapena chinachake chonga chimenecho, inu mukudziwa, kapena chirichonse chimene chabwera mmalingaliro anga. Chotero, palibe amene amadziwa pamene mzere wapempherowo ukuyambira, ndipo izi zimapereka mwayi kwa munthu aliyense. Ndiye, pamapeto ake, tonse pamodzi, ife timamupempherera munthu aliyense amene ali ndi khadi. Kotero ife. . .Mumangogwira khadi lanu.

6 Tsopano nthawi zambiri, mmisonkhano, kuti anthu samafika nkomwe pa nsanja. Ngati alipo aliyense pano, amene anayamba wakhalapo mu msonkhano m'mbuyomu; pamakhala teni kunja uko ochiritsidwa pamene mmodzi wachiritsidwa pa nsanja.

7 Zimatengera chikhulupiriro. Ziribe kanthu kumene izo ziri, iwe umayenera kukumana ndi chikhulupiriro chimenecho. Ndizo zonse. Ndipo chikhulupiriro si basi a—nthano, basi chinachake chimene iwe ukuchiganizira. Ndi chinachake chimene iwe ukuchidziwa. Uko nkulondola.

8 Ndipo tsopano ine ndikufunsani inu, tsopano, pamene ife tikutsegula tsopano pa kuwerenga kwa Lemba, usikuuno. Ife tiwerenga kuchokera mu Bukhu la—kuchokera mu Bukhu la Ahebri, usikuuno, ndipo tsopano pamene ife tikuyima kuti tiwerenge Mawu. Ife timayima pamene timalonjeza kukhulupirika ku mbendera, ndipo ife—ife timaimirira molemekeza makaka athu onse a fuko, ndi zina zotero, kotero tiyeni tiyimirire pamene tikuwerenga Mawu a Mulungu. Kodi mutero? Ahebri, mutu wa 13, ndime ya 1 mpaka 8.

> *Mulole chikondi cha pa abale chipitirire.*
>
> *Musakhale. . .kuchereza alendo: pakuti mwa ichi ena anachereza angelo* mosadziwa.
>
> *Kumbukirani iwo amene ali mu nsinga, monga* ansinga *pamodzi ndi iwo; ndi iwo amene* a*kusauka, pokhala* inumwini *nanunso mu thupi.*
>
> *Ukwati ndi wolemekezeka mu zonse, ndipo pogona pakhale posadetsedwa: koma adama ndi achigololo Mulungu adzawaweruza.*
>
> *Mulole* zoyankhula *zanu zikhale zopanda kusirira; ndipo muzikhala okhutira ndi zinthu zimene muli nazo: pakuti iye* wanena kuti, *sindidzakusiyani inu konse, ngakhale kukutayani inu.*
>
> *Kotero kuti ife tikhoza kunena molimbika mtima kuti, Ambuye ndi mthandizi wanga,. . .sindidzawopa chimene munthu adzandichitira ine.*
>
> *Akumbukireni iwo amene ali ndi ulamuliro pa inu, amene ayankhula kwa inu mawu a Mulungu: amene chikhulupiriro chawo mumachitsatira, poyang'anira chimaliziro cha* zoyankhula *zawo.*

*Yesu Khristu yemweyo dzulo,. . .lero, ndi kwanthawizonse.*

9 Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Ambuye Yesu, pangani ichi kukhala chenicheni kwa ife, usikuuno. Osati kungowerenga kwa Mawu, koma mulole kuti Mawu asandulike thupi pakati pathu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

Mukhoza kukhala pansi.

10 Pamene ife tikuyankhula kwa mphindi zochepa chabe, ndipo usiku uliwonse ife tiziyesetsa kuti tizituluka pofika hafu pasti naini, ngati—ngati zingatheke. Ine ndikufuna kuwathokoza ondithandizira anga, kachiwiri, ndi anthu amene anatilola kuti tikhale ndi malowa pano, mabwalowa, chiwonetsero cha zinthu, kapena chirichonse chimene icho chiri. Ndife othokoza kwambiri. Tsopano, tsopano ndinu gulu labwino kuyankhula nalo, ndipo ine ndikhoza kumangoyankhula kwa nthawi yayitali, koma ine sindikufuna kuti ndikutopetseni inu. Usiku uliwonse, pafupifupi maminiti sarte; usikuuno ukhala wotalikirapo pang'ono chifukwa chokhala usiku woyamba.

11 Ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa phunziro usikuuno la: *Khristu Wozindikiritsidwa Wa Mibadwo Yonse*. Chifukwa, Baibulo limati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," ndi chizindikiritso cha Khristu mmibadwo yonse.

12 Tsopano kodi inu munazindikira apa, Lemba likunena apa, kuti, "Kumbukirani iwo amene ali ndi ulamuliro pa inu; poganizira zokambirana zawo, mwaona. Pamapeto pa zokambirana zawo pali Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

13 Kotero anthu ambiri amakhala ndi malingaliro osiyanasiyana pa nkhani ya Khristu. Pamene ndikuyenda mu—mmadera osiyanasiyana a dzikoli, ndi kuzungulira dziko lapansi, ndimapeza kuti anthu ambiri amakhala ndi malingaliro awo osiyanasiyana. Inu mukhoza kudabwa mutadziwa chimene ena mwa malingaliro awo ali. Ena a iwo amaganiza kuti Iye ndi mphunzitsi wodabwitsa chabe. Chabwino, tsopano, Iye anali—Iye anali chimenecho. Ndizo ndendende basi. Ndipo ambiri amaganiza kuti Iye anali wambalume wamkulu. Chimene, Iye anali chimenecho. Iye, ndithudi, Iye anali. Ndiyeno ena a iwo amaganiza kuti Iye anali—munthu wabwino. Iye, Iye anali chimenecho. Koma, taonani, Iye anali woposa zimenezo. Iye anali zonsezo, kuwonjezerapo. Ena a iwo amaganiza kuti Iye anali mneneri. Iye anali mneneri, koma Iye anali woposa mneneri. Iye anali chimene aneneriwo anali, kuwonjezerapo. Mukuona? Kotero, chiyani, ife tingadziwe bwanji tsopano? Ngati Iye ankaphunzitsa za ziphunzitso Zake, Iye anali mphunzitsi ndipo Iye anali wambalume wamkulu.

14 Koma a—njira yokhayo imene ife tidzadziwire konse, lero, ngati ife tikanafuna kuti timuzindikiritse Iye, lero, ndipo, ine ndimakhulupirira kuti Iye anawuka kwa akufa. Ine ndimakhulupirira zimenezo ndi mtima wanga wonse. Ndipo ine ndimakhulupirira kuti Iye analonjeza apa, kuti, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." "Ndipo Ine ndiri ndi inu nthawi zonse, ndipo Ine sindidzakusiyani konse, kapena kukutayani inu."

15 Tsopano, Mawu amenewo ali, iwo mwinamwake ndi owona kapena iwo si owona. Ndipo ngati Iwo si owona, ndiye ife tikuchita chiyani pano usikuuno? Ife ndi—ife ndi anthu atsoka, ife ndi anthu amene—amene, chabwino, ife tanyengedwa; dziko lonse la Chikhristu lanyengedwa ngati Iye sali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ngati Iye sali wamoyo usikuuno ndipo nkukhala ndi ife monga Iye analonjezera. "Taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale kufikira ku chimaliziro, kapena kumapeto kwa dziko lapansi. Ndiri ndi inu nthawi zonse." Tsopano, ngati icho si Choonadi, ndiye pali chinachake cholakwika, ndipo ife tiri—ife tapezeka kukhala mboni zabodza. Sikuti tikungodzipangitsa tokha kukhala omvetsa chisoni, mwa kunamizira kwabodza, koma tikuwanyenganso ena. Ife tapezeka kukhala onyenga, a chinachake chimene ife tikuchikamba, chimene sichiri, ngati Iye ali nthano chabe kapena ngati Iye ali wambiriyakale chabe.

16 Kodi Khristu wa mbiriyakale ali ndi ubwino wanji ngati Iye siali yemweyo lero? Ndi waubwino wanji Mulungu wa Mose ngati Iye siali—siali Mulungu yemweyo lero? Izo zimachita ubwino wanji kutenga yanu—mbalame yanu ndi kuidyetsa mavitamini abwino, kuyipanga iyo kukhala ndi nthenga zokongola ndi mapiko abwino amphamvu, ndipo kenako nkuyisunga iyo mu khola? Mwaona, izo sizimaichitira iyo ubwino uliwonse. Ndipo ife tikamayankhula za momwe Mulungu analiri wamkulu, ndiyeno osanena kuti Iye ali yemweyo lero, ndiye kuti pali chinachake cholakwika. Ife tayikidwa mu khola penapake. Ndipo, izo, limenelo ndi—limenelo ndi lingaliro labodza la chimene Mulungu ali.

17 Baibulo limanena momveka kuti, "Iye ali yemweyo," ndipo zimenezo zikutanthauza kuti Iye ali yemweyo. Iye ali basi momwe Iye analiri. Iye sanasinthe ngakhale pang'ono, ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

18 Ndipo tsopano ife tiri, lero, mu tsiku lino ndi nthawi, chimodzimodzi basi monga momwe iwo anachitira mu tsiku Lake ndi mmasiku onse, ife tiri nalo lingaliro lathulathu la Izo. Koma, ndithudi, ngati pali njira iliyonse mu dziko imene ife tingadziwire moona, ife tikuyenera kupeza chimene Iye anali, ndipo kenako nkupeza chimene Iye anali mu mibadwo inayo.

19 Kumbukirani, Baibulo linati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero,

ndi kwanthawizonse." Kotero ife tikuyenera kupeza chimene Iye ali, kuchokera mmibadwo inayo; kudziwa chimene Iye anali mu m'badwo umene Iye anayenda pa dziko lapansi, m'badwo umene Iye anali asanayende pa dziko lapansi, ndi m'badwo umene Iye anali atakhala pa dziko lapansi ndipo atachoka pa dziko lapansi. Ife tikuyenera kupeza chimene Iye anali, kuti tidziwe chimene Iye ali lero, nthawizonse, chifukwa Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Tsopano, koma, mwanjira yina, ife tikuyenera kubwerera mmbuyo ndi kukafufuza, kuti tiwone chirichonse chimene Iye anali.

20 Tsopano ife tikupeza kuti, mu Yohane Woyera mutu wa 1, kuyambira ndi ndime ya 1, amati, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu." Tsopano izo ndi zikhumbo, Mawu Ake; iwo ndi malingaliro tsopano, iwo sanafotokozedwe. Onani, "Pachiyambi ziri, panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhazikika pakati pathu. Pachiyambi panali Mawu!" Chabwino, ngati Iye anali Mawu pachiyambi, Iye ndi Mawu lero, chifukwa Iye nthawizonse ndi Mawu.

Tsopano Mulungu akuyenera kuti adzaliweruze dziko lapansi ndi chinachake.

21 Ndipo anthu amati, chabwino, tsopano monga . . . Ngati ine ndingawafunse Akatolika pano usikuuno, mukuganiza kuti Mulungu adzaweruza dziko lapansi ndi chiyani? Akatolika anganene kuti, "Ndi mpingo wa Katolika." Chabwino, tsopano mpingo wa Katolika wake uti? Tsopano iwo ali ndi wa Chiroma, Greek Orthodox, ndi yambiri ya iyo. Ungakhale mpingo wa Katolika wake uti? A Chilutera amati, "Ndi ife," ndiye kuti inu Abaptisti muli kunja. Ndipo kenako ngati ife tingati, "Ndi Abaptisti," ndiye kuti inu Achipentekoste muli kunja. Kotero pangakhale chisokonezo chotero, palibe amene angadziwe choti achite, kotero Iye sanalonjeze konse kuti adzaweruza dziko lapansi ndi mpingo.

22 Iye analonjeza kuti adzaweruza dziko lapansi ndi Khristu, ndipo Khristu ndi Mawu. Ndipo Baibulo ndi lomwe lidzaweruze dziko, amene ali Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

23 Tsopano, ngati Iye anali pachiyambi, Iye anayika Mawu Ake, mochuluka kwambiri, ku m'badwo uliwonse, nthawi iliyonse imene Iye—imene Iye anali ndi m'badwo uwu ukubwerapo.

24 Iye ndi wopezeka ponseponse, wodziwazonse, wamphamvuzonse, ndipo wopanda malire. Ngati Iye siali chomwecho, Iye si Mulungu. Pokhala wopandamalire, Iye ndi—Iye ndi—Iye ndi Wamuyaya. Ndiyeno, mmenemo, pokhala wopezeka ponseponse; pokhala wodziwazonse, kudziwa zinthu

zonse, zimamupanga Iye kukhala wopezeka ponseponse. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

25 Kotero, ndiye, Iye amakhoza kudziwa mapeto kuchokera ku chiyambi, ndipo mu m'badwo uliwonse Iye anagawa zochuluka chotero za Mawu Ake, mu m'badwo uliwonse.

26 Ndiyeno, kawirikawiri, munthu amawapotoza Iwo kwambiri, ndipo dziko limafika mchikhalidwe chotero, mpaka Iye amayenera kutumiza munthu wina, wodzozedwa. Mibadwo yonse yakhala ili mofanana. Iye amadzizindikiritsa Yekha pa dziko lapansi, mwa munthu. Mulungu samachita kanthu popanda munthu. Baibulo linanena chomwecho, inu mukudziwa. Mukuona? Iye nthawizonse amamutenga munthu, chifukwa anali munthu amene Iye ankayenera kumugwiritsa ntchito, ndi kumulola munthuyo. . . Anamuyika iye pa ufulu wosankha, akudziwa kuti iye akanadzagwa, ndi cholinga choti adzawonetsere zikhumbo Zake monga Mpulumutsi, pakuti panalibe kanthu kalikonse kotayika. Ndipo, chotero, Iye anamusankha munthu. Iye akanasankha nyenyezi, Iye akanasankha mitengo, koma Iye anamusankha munthu.

27 Nthawi yina, atayima, akuyang'ana pa zokolola; Yesu, Iye anati, "Zokolola zacha. Ogwira ntchito ndi ochepa. Pemphani Ambuye wa zokolola kuti atumize antchito mu zokolola Zake." Ndipo Iye anali Mbuye wa zokolola. Mukuona? "Inu mulibe chifukwa simupempha. Simupempha chifukwa simukhulupirira. Pemphani zochuluka, kuti chimwemwe chanu chidzaze." Mukuona? Iye akudalira pa inu kuti muzipempha, ndi kuti muzikhulupirira kuti mulandira chimene mwachipemphacho.

28 Tsopano, ndiye, pachiyambi, ife tikupeza kuti Iye anagawa Mawu Ake. Ife tikupeza kuti, mmasiku a Mose ndi monse kutsika mmusi, kuti Iye—Iye ankadzizindikiritsa Yekha nthawi iliyonse mwa aneneri Ake. Baibulo limati, "Iye samachita kanthu mpaka poyamba Iye atawulula izo kwa aneneri Ake." Ndipo, kumbukirani, Mulungu ndi Mulungu wosasintha. Iye samasintha konse. Iye akadali yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

29 Tsopano ife tikupeza kuti, mu m'badwo uliwonse, kuti munthu amalowa mu dongosolo la Mulungu. Iwo amapanga malingaliro awoawo, ndipo izo zimawoneka zabwino. Izo zimawoneka zabwino, zabwino kwambiri. Ndipo nthawizina zimakhala zoyandikana kwambiri pakhoza kukhala mawu amodzi osiyanitsa, koma mawu amodzi amenewo amatanthauza kusiyana pakati pa imfa ndi Moyo.

30 Anali mawu amodzi amene anayambitsa mpira wonse uwu kugudubuzika, pamene Eva sanakhulupirire gawo limodzi la Mawu a Mulungu. Kumbukirani, iye sanati. . . Satana sanangokhala ngati wataya chinthu chonsecho. Iye anati, "Oh,

ndithudi Izi zidzakhala mwanjira iyi, ndipo Iyi ndi njira imeneyo, ndipo Mulungu wakuti-ndi-wakuti, koma ndithudi Iye sangachite *ichi*."

31 Koma Iye anati Iye akanadzachita izo, ndipo, pamene Iye anati Iye akanadzachita izo, izo zimapangitsa izo kukhala chomwecho. Mukuona? Basi, inu mukuyenera kukhulupirira gawo lirilonse la Iwo. Ziribe kanthu zomwe Iwo akunena, muwakhulupirire Iwo mulimonse. Ngati inu simungathe kuwafotokoza Iwo, muwakhulupirire Iwo mulimonse. Simungathe kumufotokoza Mulungu; palibe amene angathe. Mulungu amadziwika mwa chikhulupiriro, osati mwa sayansi. Inu mumamukhulupirira Mulungu mwa chikhulupiriro, chifukwa Iye ananena chomwecho, ndipo izo zimakhazikitsa izo. Bola ngati Iye ananena kuti Izo ziri chomwecho, izo zimachiza vutolo. Iye ananena chomwecho; sizimapanga kusiyana kulikonse momwe sayansi inganenere kuti Izo siziri.

32 Nowa, Nowa sakanakhoza kufotokoza momwe madzi analiri mu mlengalenga, chifukwa sayansi inati munalibemo mmenemo. Koma ngati Mulungu ananena chomwecho, Iye ndi wokhoza kuyika madzi mmwamba mmenemo, kotero izo—izo zinakhazikitsa izo. Mwaona, iye anangomukhulupirira Mulungu.

33 Nthawizonse, munthu amene ali wodzozedwa ndi Mawu, amakhulupirira chimene Mulungu ananena. Mosalabadira ngati iye angathe kutsimikizira izo, kapena ayi, iye amawakhulupirira Iwo mulimonse. Mulungu amachita kutsimikizirako.

34 Mvetserani, lero ife nthawizonse timakhala ngati . . . Munthu nthawizonse amamuyamikira Mulungu pa zomwe Iye anachita, nthawizonse amayembekezera pa chimene Iye ati adzachite, ndipo amanyalanyaza chimene Iye akuchita. Chakhala chiri chinthu chomwecho nthawizonse. Ndipo aliyense ali ndi kutanthauzira kwake kwake.

35 Mulungu ndi wodzitanthauzira Iye Mwini. Mulungu samasowa winawake kuti amutanthauzire. Baibulo linati Ilo ndi lopanda kutanthauzira. Ilo silisowa munthu. Mulungu amatanthauzira Baibulo, Mwiniwake. Mulungu anati, "Pakhale kuwala," ndipo panali kuwala. Izo zinakhazikitsa izo. Mulungu anati, "Namwali adzayima," ndipo iye anatero. Izo zinakhazikitsa izo. Pamene Mulungu anena chirichonse, ndi kuchitsimikizira icho, uko ndiko kutanthauzira Kwake kwa izo. Iye anati Iye akanadza "tsanulirani Mzimu Wake" mmasiku otsiriza ano, ndipo Iye anachita zimenezo. Palibe kutanthauzira kwa izo; izo zinatanthauziridwa kale. Osakhulupirira akhoza kuwuka, ndipo okayikira akhoza kuyima, ndi chirichonse chimene iwo angakhoze kuchita; koma Mulungu anachita izo, mulimonse, chifukwa Iye anati Iye akanadzachita izo. Iye samasowa aliyense kuti amutanthauzire Iye. Iye amachita

kutanthauzira Kwake Mwiniwake. Iye anapanga lonjezo, anthu amalikhulupirira ilo, ndipo Iye amalitanthauzira ilo kwa iwo.

36 Iye ndi Ambuye amene amachiritsa matenda athu onse. Ine sindingakuuzeni inu momwe Iye amachitira izo, koma Iye amachita zimenezo. Iye anati Iye akanadzachita izo, kuti Iye akanadzachita izo, kotero izo ziri kwa chikhulupiriro chathu. Iye sakanakhoza kuchita izo kumeneko popanda chikhulupiriro, Iye sangakhozenso kuchita izo pano, kapena nthawi iliyonse, popanda chikhulupiriro.

Tsopano, Iye ndi Mawu. Iye ndi Mawu ozindikiritsidwa ku m'badwo umenewo.

37 Tsopano, vuto ndi anthu, lero, ife tikuwapeza iwo akukhala mu kunyezimira kwa m'badwo wina. Monga momwe Yesu anawapezera pamene Iye anabwera, Iye anawapeza iwo akukhala mu kunyezimira kwa chilamulo, ndi kumanyalanyaza zomwe zikanati zidzachitike mu m'badwo Wake. Inu mukudziwa limene liri vuto lero? Chavuta ndi chiyani ndi . . .

38 Kodi vuto linali chiyani ndi Achilutera? Chabwino, chifukwa iwo ankakhala mu kunyezimira kwa m'badwo wa Chilutera, pamene John Wesley anapeza chinsinsi cha kuyeretsedwa, iwo sanathe kuti azipitirira, chifukwa iwo ankakhala mu kunyezimira kwa m'badwo wa Luther.

Kodi chinachitika ndi chiyani kwa Achipentekoste?

39 Bwanji, Wesley anali wabungwe kwambiri, mpaka iye ankakhala mu kunyezimira kwa m'badwo wina, iwo anali mu m'badwo wa Wesley, pamene ubatizo wa Mzimu Woyera unagwera pa Achipentekoste. Mwaona, iwo ankakhala mu chimene Wesley ankati, kuyeretsedwa. Izo zinali zovuta kwa iwo kuti akhulupirire ubatizo wa Mzimu Woyera, kubwezeretsedwa kwa mphatso. Iwo ankakhala mu kunyezimira kwa m'badwo wina.

40 Ndipo icho ndi chimene iwo ankachita pamene Yesu anabwera. Anati, "Ife tiri naye Mose. Ife, ife tiri naye Mose."

41 Iye anati, "Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanandidziwa Ine. Mose analemba za Ine. Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mumaganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ndi Amene akuchitira umboni za Ine." Limenelo linali Lemba limene linkayenera kukhala.

42 Mulungu akuzindikiritsa, akutanthauzira Lemba Lake la m'badwo umenewo, ndipo nthawizonse ndi Khristu. Ndi Khristu mu m'badwo uliwonse. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Wakhala ali Khristu nthawizonse.

43 Tsopano ife tikupeza kuti, kuti tsopano ife tikupeza abale athu Achipentekoste akukhala mu kunyezimira kwa m'badwo wa Chipentekoste, ndipo iwo akuchiphonyabe Icho.

Iwo akuyesetsa kutanthauzira m'badwo wa Chipentekoste, pamene ife tinadutsa zimenezo. Ife tikukhala mpaka ku nthawi ya mkwatulo, ya kudza kwa a—nthawi yakumapeto. Koma umo ndi momwe munthu amachitira, amangokhala mwanjira imeneyo.

44 Ife tiri ndi ochuluka kwambiri amene anaperekedwa ku m'badwo uliwonse. Baibulo linaperekedwa mwanjira imeneyo, ndipo umo ndi momwe ife tikuyenera kukhalira nalo ilo. Umo ndi momwe izo zikuyenera kukhalira.

45 Mulungu wosasintha, wokhala ndi khalidwe losasintha, ndipo makhalidwe Ake amakhalabe omwewo. Iye sangasinthe khalidwe Lake. Iye sangachite zimenezo. Chirichonse chimadziwika ndi chikhalidwe chake.

46 Ine sindikudziwa ngati inu nonse muli ndi mpheta kumusi kuno kapena ayi, katawa . . . timazitcha izo "zaliwiro," ndi a—katawa. Izo zonse ziwiri ndi za pafupifupi msinkhu wofanana. Inu mudzamuwone katawa akuwuluka, ngati iye ali patali ndipo mudzamuyang'ane iye, iye amapanga mzere wa B pamene akuwuluka. Koma, mpheta, iyo imapita mmwamba-ndi-pansi pamene ikuwuluka. Mwaona, icho ndi chikhalidwe cha mpheta. Mukhoza kuyidziwa iyo ndi machitidwe ake.

Mudzamuwone munthu yemwe amagwiritsa ntchito dzanja lake lamanja kapena lamanzere. Iye ndi khali- . . .

47 Ife tiri nawo akazi lero amene amafuna kuti akhale amuna. Iwo amavala ngati iwo, koma iwo akadali . . . Mudzawawone iwo akamayenda ndi zomwe iwo amachita, iwo akadali . . . Khalidwe lawo limawonetsera kuti iwo ndi akazi, komabe, mofanana basi, mwaona, chifukwa izo basi zimakhala mwanjira imeneyo. Ife tifika kwa zimenezo patsogolo. Koma, komabe, ife tiri pa chinthu china pakali pano.

Kumbukirani, iwe umazindikiritsidwa ndi khalidwe.

48 Ndipo Mulungu amazindikiritsidwa ndi khalidwe Lake lalikulu, limene, "Iye sangalisinthe." Iye ananena, mu Malaki 3:6, "Ine ndine Mulungu, ndipo Ine sindimasintha." Mukuona? Iye mwamtheradi samasintha. Makhalidwe Ake ndi omwewo.

49 Nthawi iliyonse imene Iye anawonekera pa dziko lapansi, pa mapeto a m'badwo, Iye nthawizonse wakhala akutumiza munthu ndi kumudzodza iye ndi Mzimu Woyera, Khristu. Mzimu Woyera ndi Khristu, "wodzozedwayo," *Logos*, ndipo Iwo unkatuluka, ndipo Iwo unkabwera kudzazindikiritsa a—Mawu a m'badwo umenewo. "Mawu a Ambuye amadza kwa aneneri," Baibulo linanena chomwecho, ndipo amazindikiritsa m'badwo umenewo. Mwaona, Iye samachita kanthu kunja kwa munthu. Tsopano Iye sangachite izo mu gulu. Inu simungathe kuchita izo. Izo sizinayambe zachitikapo basi. Iye sanayambe wagwiritsapo ntchito gulu; sanayambe wachitapo. Iye amagwiritsa ntchito munthu m'modzi. Inu simuli . . .

50 Israeli anapulumutsidwa ngati fuko, koma inu mudzapulumutsidwa ngati munthu panokha.

51 Ndipo Iye amachita ndi munthu mmodzi. Iye anali ndi. . .Iye analibe ngakhale a—a—a Mose ndi Eliya, nthawi imodzi. Iye sakanakhoza kukhala ndi Eliya ndi Elisha, nthawi yomweyo. Iye sakanakhala ndi Yohane ndi Yesu, nthawi imodzi. Iye nthawizonse wakhala ali ndi mmodzi, chifukwa Iye amamutengera munthu mmodzi ameneyo mu chifuniro Chake Chauzimu.

52 Ngati ife titayamba usikuuno, ndipo ine nditatenga munthu mmodzi, mwamuna wina pano amene ine ndingamusankhe, ndipo ife nkugwirizana pa chiphunzitso, mwangwiro basi, ife tikhoza kuyambitsa gulu laling'ono. Patatha chaka kuchokera lero, ife tingakhale ndi ma Ricky ochuluka mmenemo, bwanji, izo zingakhale zamanyazi. Uko nkulondola, iwo angangobweramo ngati tizirombo. Inu simungakhoze kuwaletsa iwo. Chotero, chomwecho, ako sikanakhalepo kachitidwe ka Mulungu.

53 Mulungu sangasinthe. Iye amachita, chimodzimodzi, ndi munthu mmodzi! Iye anachita izo kudutsa mmibadwo. Iye wakhala akuchita izo nthawizonse.

54 Ndipo khalidwe Lake limazindikiritsidwa ku m'badwo umenewo. Tsopano, musaiwale zimenezo, khalidwe Lake limazindikiritsidwa mu m'badwo umenewo.

55 Taonani mmasiku a Yosefe, mneneri, momwe Yesu anazindikiritsidwa mwangwiro mwa Yosefe. Iye anabadwa, wokondedwa ndi atate wake, wodedwa ndi abale ake, popanda chifukwa. Iye ankawakonda abale ake. Koma iwo anali Achifarisi odzitukumula, monga, ndipo iwo analibe kanthu kochita ndi iye, ndipo ankamuda iye chifukwa ankawona masomphenya ndi—ndi zina zotero. Koma khalidwe lomwe mwa iye linkawonetsera kuti anali Khristu.

56 Yosefe anali mneneri. Iye ankaneneratu zinthu. Izo zinkachitika chimodzimodzi basi momwe izo zinachitikira. Momwe iye anayankhulira izo, umo ndi momwe izo zinkachitikira. Ndipo iye ankatanthauzira maloto, ndipo iye sankangopereka kutanthauzira kopanda pake kwa iwo. Nthawi iliyonse imene iye ankanena kuti zikanadzakhala chomwecho, umo ndi momwe izo zinkakhalira basi. Iye anabadwa, mneneri, ku m'badwo umenewo. Kulondola ndendende. Tsopano, ife tikupeza kuti Mulungu anawonetsera khalidwe Lake mwa Yosefe.

57 Aliyense wa aneneriwo anawonetsera khalidwe la Mulungu, chifukwa ilo linkatenga Mawu a m'badwo umenewo ndi kuwazindikiritsa iwo. Mulungu ankatanthauzira Mawu Ake, a m'badwo umenewo, kupyolera mwa munthuyo. Tsopano, palibe amene angapeze cholakwika ndi zimenezo. Limenelo ndi Lemba.

58 Chabwino, ngati izo zakhala ziri mwanjira imeneyo nthawizonse, kodi izo sizikuyenera kukhala chimodzimodzi lero, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse?

59 Mulungu ankatanthauzira Mawu Ake Omwe! Iye anati, "Chinthu *ichi* chidzachitika mu m'badwo winawake, ndipo chinthu *ichi* chidzachitika," ndipo Iye amabwera pansi ndi kudzachichita icho. Tsopano, Iye samasowa kutanthauzira kwa icho, chifukwa icho chimachita chokha. Iye samasowa aliyense kuti amutanthauzire Iye. Iye ndi Elohim, wokhalapo-Yekhayo, *Wokwanira Muzonse*. Iye samasowa kuthandizidwa ndi aliyense. Mwaona, Iye ndi Mulungu, ndipo Iye amachita monga Iye akufunira.

60 Ndipo pali chinthu chimodzi chimene ife tiri otsimikiza kuti Iye sangathe kuchichita; Iye sangapite motsutsana ndi Mawu Ake, ndi kukhalabe Mulungu. Iye akuyenera kusunga Mawu Ake, chifukwa Mawu ndi Mulungu. Iwo ndi . . . Ndipo Mulungu amazindikiritsidwa kudzera mu Mawu Ake olonjezedwa pa m'badwo.

61 Mu enaake, mmasiku a . . . tsopano, bwanji mmasiku a Mose? Iye anazindikiritsidwa. Iye anazindikiritsidwa chifukwa Iye anazindikiritsidwa ndi Mawu Ake. Iye anamuuza Abrahamu, "Mbewu yako idzakhala m'dziko lachilendo kwa zaka foro handirede. Ine ndidzawatulutsa iwo ndi dzanja lamphamvu."

62 Tsopano, pamene chizindikiro chachikulu ichi chinachitika, ngati mpira wawukulu wa Moto mu chitsamba chonyeka, Mose anali wa zamankhwala, iye anaphunzitsidwa mu nzeru zonse za Aigupto, bwanji ngati Mose akanapita ndi ake—ndi mayimidwe ake a maphunziro, ndikuti, "Tayang'anani pa mtengo woseketsa uwo! Iwo ukuyaka moto. Iwo ukunyeka. Masamba akuphulika, ndipo palibe chimene chikuwonongeka, chikunyeka. Tsopano, icho chikatha kuyaka, ine nditola ena a masamba amenewo ndipo ndipita nawo ku labotare ndi kukafufuza kuti ndi mtundu wanji wa mankhwala amene anapoperedwapo"? Icho sichikanayankhula nkomwe kwa iye! Koma pamene iye anavula nsapato zake, anayenda modzichepetsa!

63 Umo ndi momwe ife timamupezera Mulungu, pamene tichotsa kunyada kwathu ndi kukuyika iko pansi, ndi kuyenda kupita mu Kukhalapo.

64 Kumvetsera ku liwu limenelo likuzindikira. "INE NDINE AMENE INE NDIRI. Ine ndine Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo. Ine ndakumbukira lonjezo Langa, ndipo Ine ndikuwona kuti chikhalidwecho chiri molondola. Ine ndatsika pansi, ndipo Ine ndiyankhula. Ndipo Ine ndikukutuma iwe, ndipo iwe ukakhala liwu Langa." Oh, mai!

65 Umo ndi momwe Iye amachitira izo. Kodi Iye anachita izo motani? Podzizindikiritsa Yekha mu chikhalidwe Chake, mu chauzimu. Chauzimu nthawizina chimakhala chodabwitsa

kwambiri, Icho chimawadutsa anthu kutali kwambiri. Anthuwo amakhala anthu abwino, okoma, koma nthawizina iwo samamvetsetsa.

66 Icho ndi chimene, icho chinali chinthu chomwecho ndi Yosefe. Iye sankamvetsa. Iye anali mwana wa Davide, koma iye sankamvetsa momwe Mariya anakhalira ndi pakati. Tsopano, mosakayika, ndi maso aakulu amenewo, abulauni okongola, anayang'ana pa nkhope yake, ndipo anati, "Wokondedwa, ine ndikudziwa kuti tinatomerana kuti tikwatirane. Ine ndiri ndi chinachake choti ndikuwuze iwe. Ine ndinachezeredwa, ndi Gabriel, ndipo ine ndiri . . . Ndiri ndi pakati, 'pa Mzimu Woyera,' Iye anandiuza ine. 'Ndipo chinthu ichi chimene chidzabadwe sichidzakhala mwana wako; adzakhala Mwana wa Mulungu.'" Ndipo, tsopano, Yosefe ankafuna kuti akhulupirire zimenezo. Koma iye—iye sankakhoza kukhulupirira izo, basi. Zinali zovuta kwambiri kwa iye kuti akhulupirire. Koma, inu mukudziwa, izo zinali zachilendo. Akazi sankatenga pakati, mwaunamwali, kotero izo zinali zachilendo.

67 Ndipo izo ndi zinthu zosazolowereka zimene Mulungu amachita. Zimawapunthwitsa anthu. Izo zimawalitsa, zimatsegula maso a ena, ndi kuchititsa khungu ena, pa nthawi yomweyo. Izo nthawizonse zakhala zikuchita zimenezo, Iye— Iye, zinthu zachilendo ndi njira yachilendo.

68 Ngati Yosefe akanangoyang'ana mu Lemba, kuti apeze zomwe zikanati zidzachitike mu tsiku limenelo. Tsopano, kunalibe aneneri nthawi imeneyo. Iwo anali asanakhale ndi mneneri kwa zaka foro handirede. Malaki anali mneneri wawo wotsiriza. Ndipo aneneri anali achilendo kwambiri. Kotero iwo analibe aneneri mmasiku amenewo, kotero Mulungu anatenga chachiwiri, ndipo anamupatsa iye loto, ndipo anamuuza iye. "Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope kudzitengera kwa iwe Mariya mkazi wako, pakuti icho chimene chiri mwa iye, mwa iye, ndi cha Mzimu Woyera."

69 Mwaona, Mulungu akudzizindikiritsa Yekha, Iye nthawizonse amachita izo mwanjira yauzimu.

70 Tsopano, awa, Yosefe ndi Mose, ndipo ngati ife tikanangokhala ndi nthawi yochuluka ife tikanakhoza kumangopitirira ndi kumapitirira ndi izo. Koma inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza, kuti, Mulungu, mu m'badwo uliwonse, nthawizonse amatumiza munthu payekha, munthu mmodzi.

71 Kotero nchifukwa chiyani inu mumangokakamira ku gulu linalake, pamene iwo onse pamodzi akulakwitsa? Baibulo linanena chomwecho, Chivumbulutso 17, izo zonse zidzasonkhanitsidwa mu gulu limodzi lalikulu. Koma kuchokera mmenemo mudzabwera anthu apawokha amene ali olondola ndi Mulungu, osati gulu lolondola; munthu payekha wolondola,

munthu payekha mu gululo. Tsopano ife tikupeza kuti, ndiye, ife timakangana ndi kumapitirira, za, “Ife ndi a *ichi*, ndipo ife ndi a *icho*.” Izo sizimatanthauza chinthu chimodzi kwa Mulungu.

72 Ndi inu ngati munthu payekha, pamaso pa Mulungu. Ngati . . . Inu mukuyenera kuyima pa mapazi anu. Ndinu amene mukuyenera kupanga umboniwo. Aliyense wa inu akuyenera kuti achite zimenezo, kuyankha kwa Mulungu chifukwa cha Vumbulutso.

73 Tsopano bwanji ngati ine ndikuyankhula pano kwa munthu amene kwenikweni sangakhoze kuwulandira Iwo, mulibemo chirichonse mwa iye choti alandirire nacho? Baibulo linati, “Iye amene amakhala mu zosangalatsa ndi wakufa pamene iye ali ndi moyo.” Nchifukwa chiyani sanali Afarisi amenewo?

74 Tayang’anani pa Yesu, zonse zomwe ife timazidziwa, Iye anali Mawu owonetseredwa a Mulungu. Ife timakhulupirira zimenezo. Baibulo linati izo zinali. Chabwino, penyani pamene Iye anachita chizindikiro Chake cha Umesiya.

75 Afarisi, amene anali ndi kuwala pang’ono. Iwo anali anthu abwino, ankakhala moyo wabwino wa Chikhristu, kapena moyo wabwino wachipembedzo, anali ndi kuwala pang’ono pa iwo. Iwo anapanga bu- . . . bungwe, ndi unsembe. Iwo anali ndi kuwala pang’ono. Koma pansi mu mtima mwawo, iwo analibe choyimirira Chamuyaya mu Ulemelero. Kotero pamene iwo anawona chauzimu icho chikuchitidwa, iwo anati, “Munthu uyu ndi Belezebule, mdierekezi.” Ndipo chinachitika ndi chiyani? Izo zinazimitsa kuwala kumene iwo anali nako.

76 Koma apa panali mayi wamng’ono, wa mbiri yoipa, hule. Pansi mumtima mwake, chabwino, iye anali ndi choyimirira cha amodzi mwa malingaliro a Mulungu. Apo iye anali, wolemetsedwa mu tchimo. Koma pamene iye anawona izo zikuchitika, iye anati, “Bwana, ine ndikukhulupirira kuti Inu ndi mneneri. Ine ndikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera Iye adzatiuza ife zinthu izi.” Kodi izo zinachita chiyani? Zinayeretsa moyo wake. Iye anali Muwomboli, kwa iye, chifukwa Iye anakhoza kumukwezera iye kumwamba kumene iye anachokerako.

77 Koma Mfarisi uyu, taganizani za zimenezo, wachipembedzo monga iye akanakhalira, ndipo Yesu anati, “Iwe ndi wa atate ako mdierekezi, ndipo ntchito zake iwe udzazichita.” Munthu wachipembedzo, anali wa makhalidwe abwino, apamwamba. Ndipo Yesu anawatcha iwo, “Njoka mu udzu, ndi adierekezi.” Iwo anakana Kuwala kwa oralo. Ndicho ndendende chimene chinali.

78 Yesu mu m’badwo Wake, kodi Iye anali chiyani? Monga aneneri a m’badwo wawo, aliyense wa iwo anali Mawu a Mulungu akutanthauziridwa kwa m’badwo umenewo.

79 Mose anali Mawu a Mulungu, otanthauziridwa. Mulungu anati, “Ine ndikutumiza iwe kumusi uko, ndipo Ine ndikawapulumutsa iwo. Ine ndikukutumiza iwe kumeneko ndi Mawu Anga. Ine ndikachita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa.” Iye anakachita zimenezo.

80 Mariya, iye anali Mawu a Mulungu, otanthauziridwa. “Namwali adzayima.” Amenewo anali Mawu a Mulungu, otanthauziridwa.

81 Tsopano apa pakubwera Yesu pa chochitika, Mulungu wa aneneri. Ndipo apa iwo anali, opangidwa bungwe kwambiri komanso atsankho, ndipo, oh, mu chikhalidwe choterocho mpaka iwo sanathe nkomwe, iwo sanamuzindikire Iye nkomwe. Iye sanabwere momwe iwo ankaganizira kuti Iye ankayenera kubwerera. Iwo ankaganiza kuti Mulungu akanakoka chotchinga chaching’ono *apa*, ndi kutsitsa makonde a Kumwamba pansi, ndipo Iye akanakhoza kutulukira ndi kudzati, “Kayafa, mkulu wansembe wa Mulungu, Ine ndafika.”

82 Koma Iye anali ndi Mwana wobadwira modyera ziweto, kumusi mu a—mphanga yaing’ono, mkhola ku Betelehemu. Kumusi uko, ali ndi udzu ndi manyowa a m’khola, mwana wamng’ono atakutidwa mu nsalu yapagoli, ndipo anakamuyika Iye modyera ziweto. Analibe maphunziro. Mukuona momwe iwo anawakonzera Mawu? Monga, Iye anali Mawu. Iye ndi Mawu. Iye adakalibe yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Kulondola.

83 Tsopano, ine sindikupanga chirichonse, kugenda kulikonse, pa aliyense kapena chirichonse. Izo siziri mu cholinga changa kuti ndichite zimenezo. Ngati izo zinali mu mtima mwanga, ine ndikanapita mozungulira kutsogolo kwa guwa ili, ndi kukakonza, choyamba.

84 Koma, taonani, kwa anthu inu amene mumapemphera kwa Mariya, ngati wopembedzera; tayang’anani pa Mariya. Ine ndimakhulupirira kuti iye anali mkazi waunamwali, ndithudi, koma iye anangokhala chofungatira chabe chimene Mulungu anachigwiritsa ntchito kuti amubweretse Khristu ku dziko lapansi. Nyumba imene . . .

85 Mulungu anatambasula chihema Chake, kuchokera pokhala Yehova, nkudzakhala munthu. Iye anali *Emmanuele,* “Mulungu akukhala pakati pathu,” kudzamanga msasa ndi ife; Mulungu, anagwiridwa mthupi; Mulungu, anadzakhala mu hema wotchedwa munthu, ameneyo anali Mwana wa Mulungu.

86 Tayang’anani pa Mariya. Apa pali Mnyamata, wa usinkhu wa zaka thwelovu, sanakhalepo ku sukulu kwa tsiku limodzi nkomwe, monga momwe ife tikudziwira; apa Iye ali, atayima mu kachisi, akutsutsana ndi ansembe. Ndipo penyani, apa pakubwera abambo ndi amayi awa, masiku atatu ndi mausiku, Iye anali atawasowa iwo, ndipo anakamupeza Iye

mu kachisi. Iwo anati, "Mwana, ife takufunafuna . . . " Mariya, mvetserani kwa Mariya, anati, "Ife, abambo ako ndi ine takhala tikukufunafuna Iwe, usana ndi usiku, ndi misozi." Tayang'anani apo, akukana umboni wake. Iye anamuuza Yosefe kuti Mzimu Woyera unamuphimba iye; iye anawauza ansembe aja kuti Uyu anali mwana wobadwa mwa namwali; ndipo apa iye wayima, ndipo akuti, "Abambo ako, Yosefe, ndi ine." Mukuona momwe izo ziriri zolakwika?

87 Koma penyani Mawu a Mulungu, anati, "Kodi inu simukudziwa kuti Ine ndikuyenera kukhala pa ntchito ya Atate Anga?" Mawu nthawizonse amakonza cholakwikacho pomuzindikiritsa Mulungu pakati pawo. Mwana wa zaka thwelovu, ngati iye akanakhala, Yosefe akanakhala atate Ake, Iye akanakhala akumanga nyumba ndi makabati. Koma Iye anali kunja uko akuphwasula zipembedzo izo za tsiku limenelo. Iye anali pa ntchito ya Atate Ake. Mukuona chimene Iye ankachita? "Ndipo kodi inu simukudziwa kuti Ine ndikuyenera kukhala pa ntchito ya Atate Anga?" Mwaona, anawauza amayi Ake, mukuona momwe izo . . .? Chabwino, Iye anali Mawu.

88 Iye ndi Mawu, ndipo Mawu amakonza cholakwikacho pozindikiritsa khalidwe la Mulungu. Ameni. Penyani, pamene dziko . . .

89 Ine ndikukhoza kumulingalira Simoni Petro. Ine ndinawerengapo nkhani yaying'ono kamodzi, ya iye ndi—ndi m'bale wake, Andreya. Ndipo dzina lake linali Simoni nthawi imeneyo, inu mukudziwa, ndipo iye anali asanatchulidwepo kuti Petro apobe. Kotero iye ndi m'bale wake anali asodzi, ndi abambo awo, ndipo iwo anali uko pa nyanja. Ndipo mwamuna wachikulireyo anali akukalamba, ndipo iye anawayitanira iwo ku ngalawayo, usiku wina, ndipo iye anati, "Anyamata, inu mukudziwa kuti ife takhala tikumudalira Mulungu. Nthawi zambiri timatha kusowa chakudya, ndipo timakhala ndi ngongole zoti tilipire. Ndipo—ndipo ife timatha kupita kunja uko, osagwira kanthu, kwa masiku awiri kapena atatu. Ndipo amayi anu ndi ine, pamaso panu . . . iwo anapita, bwanji, ife tonse timasonkhana pamodzi ndi kupemphera, ndipo Mulungu amatha kutipatsa ife nsomba zambiri. Anyamata, ine ndakhala ndikumudalira Mulungu, moyo wanga wonse. Ndipo ine nthawizonse ndinkakhala monga Mhebri woona aliyense, kuti ndidzamuwone Mesiya akubwera. Tsopano, anyamata, ine—ine ndikukalamba kwambiri tsopano. Ine mwinamwake sindidzamuwona Iye, koma ine ndikufuna kuti inu anyamata mulangizidwe bwino."

90 Ine ndikutha kumuwona iye akuyika manja ake momuzungulira Simoni, ndipo lina momuzungulira Andreya, ndipo akuti, "Anyamata, kudza Kwake kusanachitike, inu mudzawona zabodza. Padzakhala mitundu yonse ya zinthu zabodza zikuwuka, kotero izo zidzangochititsa khungu

maso a anthu." Nthawizonse zimachita zimenezo; ndipo izo zinadzakhala chomwecho basi. "Padzakhala mitundu yonse ya . . . Koma, kumbukirani, inu musadzanyengedwe. Mesiya adzakhala mneneri. Chifukwa, Mose anati, mu Deuteronome mutu wa 18, ndime ya 15, 'Ambuye Mulungu wanu adzawutsa Mneneri wonga ine.' Tsopano, ife sitinakhale ndi aneneri aliwonse oti adzawonetsere Mawu a Mulungu. Pakhala palibe aliyense wa iwo pano woti Mawu abwerepo, chotero ife tinangokhala ndi zochitika zachipembedzo kwa mahandirede ndi mahandirede a zaka. Koma pamene Mmodziyo adzafike powonekera, inu musadzanyengedwe, Iye adzakhala mneneri. Ambuye adzadzizindikiritsa Yekha. Iye adzakhala mneneri. Ndipo, pamene Iye adzabwera, Iye adzadzizindikiritsa Yekha ngati mneneri."

91 Ine ndikukhoza kulingalira tsiku lina Simoni akupita kumusi kukamuwona Yesu kumeneko pa gombe. Ndipo pamene iye anayenda kupita mu Kukhalapo kwa Yesu, Yesu anayang'ana pa iye ndipo anati . . .

92 Anangoyamba kumene utumiki Wake, tsopano, Yohane Woyera mutu wa 1, ndi pambuyo pa "Mawu anasandulika thupi ndipo anakhazikika pakati pathu," apa Iye ali. Tsopano, ife timawuzidwa kuti Andreya anamuwona Iye poyamba, ndipo anamumva Yohane akulalikira, ndipo anayesetsa kuti amutenge Simoni kuti apite. Ndipo iye basi, "Oh, chabwino, ndi mlaliki wina chabe. Zisiyeni izo zipite. Ndipo pakhala pali *ichi, icho,* kapena *chinacho*." Koma, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iwo anaganiza kuti abwere kudzawona.

93 Iye anati, "Tsopano Mesiya wafika!" Oh, Andre . . . Simoni sanakhulupirire zimenezo.

94 Kotero iye anangoyenda tsiku lina kupita pamene Yesu anayima. Yesu anali atayima panyanja m'mawa umenewo, ndipo anthu onse anali atasonkhana. Ndipo akazi anatsuka mbale mwamsanga kwenikweni, ndipo anasunga zovala zawo mmbuyo, ndi chirichonse chimene iwo sakanachapa tsiku limenelo, anabwera kumusi kuti adzamumve Iye akuyankhula. Simoni anali atawedza usiku wonse kumeneko, ndipo mwinamwake anali asanaphe nsomba kapena kanthu. Anatulukira, anaganiza, "Ine ndikukhulupirira ine ndikangomva chimene Iye akunena." Iye anayenda kupita kwa Iye.

95 Iye anali Munthu wowoneka mosamvetsetseka chotero. Baibulo linati, "Palibe kukongola kumene ife tikanayenera kumukhumbira Iye." Iye sankawoneka ngati mfumu.

96 Kukongola ndi kwa mdierekezi, nthawizonse. Uko ndi kulondola ndendende. Ndipo ife tikhoza kufika ku zimenezo, kanthawi kena patsogolo, kotero kuti tidzafufuze. Ife tikuwona chimene Kaini anapereka, ndipo tikuwona chimene chinali Kumwamba, ndipo tapeza chimene dziko ili, kukongola

kwachabe kuli, ndi chiyani. Hollywood yatenga ulamuliro, lero, ngakhale mpingo. Inde, bwana. Ndi lingaliro labodza, la mdierekezi.

97 Pakati pa kukongola kwa Ambuye, mu chiyero ndi Mphamvu; osati mu penti, ndi pawudala, ndi akabudula, ndi china chirichonse chimene iwo akuyesetsa kuti azivala ndi kuchita izo. Izo ziri mu kukongola kwa chiyero ndi chirungamo. Ife sitiri a dziko lino. Ife ndi ochokera ku ufumu umene uli Kumwamba, kumene kumakhala chirungamo. Inde.

98 Iwo sadzazikongoletsa okha ndi Zimenezo. Televizyoni yochuluka kwambiri, ndi zina zotero.

99 Kotero ndiye ife tikupeza kuti Simoni anayenda kupita mu Kukhalapo Kwake, ndipo pamenepo panayima Mmodziyo amene Andreya ankakhulupirira kuti anali Mesiya. Ndipo pamene Yesu, mwamsanga pamene Iye anayang'ana pa—pa Simoni, Iye anati, "Dzina lako ndi Simoni, ndipo ndiwe mwana wa Yonasi." Iye anadziwa pamenepo Amene iye anali. Panalibe nthabwala kuti apo panali Mulungu akuzindikiritsidwa kachiwiri pomwe pano mu Lemba, khalidwe Lake lomwelo.

Ngati Yosefe akanangoyang'ana kumbuyo uko ndi kuwona zimenezo!

100 Yesu, pamene Iye ankalalikira pano pa dziko lapansi, Iye anati. . .Iye anati, "Fufuzani Malemba, mwa Iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya; Iwo ndi Amene akuchitira umboni za Ine." Ngati iwo akanangotembenuka kuchoka ku lamulo. Lamulo linali kuchokera tsiku limenelo, ndipo iwo ankakhala mu mtundu umenewo wa kunyezimira. Koma apa iwo ali lero, iwo sankakhoza kuliwona Lemba likuzindikiritsidwa apo pomwe. Ndipo iwo analephera kuti aliwone Ilo.

101 Ndipo iwo azichita izo mu m'badwo uliwonse, ndipo iwo azichita izo mu uwu, nawonso. Palibe china choti iwo achite. Zinanenedweratu kuti iwo akanadzatero, kotero iwo—iwo adzazichita izo. Palibe njira yozizungulira izo. M'badwo wa Laodikaya udzachita chinthu chomwecho.

102 Tsopano muwoneni iye. Pamenepo iye anayima pamenepo, ndipo iye anati, "Tsopano, ife sitinakhale ndi mneneri kwa zaka foro handirede, ndipo apa pali Munthu Amene akundiuza ine yemwe ine ndiri, ndi yemwe bambo anga aumulungu anali. Ameneyo ndi Mesiya." Tsopano, timauzidwa kuti Simoni anali mbuli ndi munthu wosaphunzira, koma iye anapangidwa kukhala mutu wa Mpingo.

103 Ife tikupeza kuti, apo panali mmodzi atayima pamenepo, dzina lake—a Filipo, ndipo iye anawona zimenezo. Ndipo iye anali atakhala ndi maphunziro a Baibulo ndi mwamuna wina wotchedwa—wotchedwa Nataniele. Ngati inu mungazindikire pamene Yesu anali, kukafika kumene iye anamupeza Nataniele,

iwo anali mailosi fifitini. Umenewo ndi ulendo wa tsiku labwino. Kotero iye akuyenera kuti anathamangira kumeneko, anazungulira phiriro, monga choncho. Tsopano ife tikawona. Iye anati, "Nataniele!" Pamene iye anakumana naye, iye anati, "Iwe ukudziwa, ife takhala tiri ndi maphunziro a Baibulo."

"Inde."

104 "Chabwino, tsopano, ife takhala tikukhulupirira kuti ndi nthawi yoti chinachake chichitike. Nyengo zikusintha, ndipo ife tiri mu nthawi yoti Mesiya abwere, chifukwa ife sitinakhale ndi mneneri aliyense tsopano kwa zaka foro handirede. Ndipo Malaki anatiuza ife kuti Iye akanadzatumiza wotsogolera patsogolo pathu, ndipo ine ndikukhulupirira kuti ameneyo ndi Yohane."

105 Tsopano ife tikudziwa, pamene inu muwona chizindikiro, chizindikiro choona cha Baibulo, pamakhala liwu loona la Baibulo kuseri kwa icho. Ngati palibe liwu limene likutsatira chizindikirocho, basi liwu lakale lomwelo la maphunziro azafioloje, iwalani zimenezo; icho sichinabwere kuchokera kwa Mulungu. Pamakhala, nthawizonse. Anamuuza Mose, "Ngati iwo sakakhulupirira chizindikiro choyamba, iwo akakhulupirira liwu la chizindikiro chachiwiri." Pamayenera kukhala liwu ndi chizindikiro. Mwamtheradi! Ndipo ngati ilo liri liwu la maphunziro azafioloje lakale lomwelo, muiwale zimenezo. Inu munali nazo izo kale. Icho ndi chinachake; Mulungu akuyesetsa kukopa tcheru cha anthu, mwa chizindikiro, ndipo kenako nkuwapatsa iwo liwu, limene liri kuseri kwa chizindikirocho. Likuyenera kukhala liwu la Mwamalemba; Mose sakanakhulupirira izo, ngakhalenso Paulo.

106 Pa ulendo wake waku Damasiko, pamene iye anawona chizindikiro chimenecho, cha Lawi la Moto lija, iye anafuula mokweza, "Ambuye!" Myuda ameneyo sakanatchula china chirichonse "Ambuye," koma Ambuye, koma Ambuye Mwiniwake. Iye anati, "Inu ndi Ndani?"

107 Iye anati, "Ine ndine Yesu, ndipo nkovuta kwa iwe kuti uzimenyana ndi zisonga." Mukuona? Apo panali chizindikirocho, ndipo apo panali liwu la chizindikirocho.

108 Ndiye tayang'anani chimene iye ananena. Tayang'anani, taonani utumiki wake kuyambira pamenepo mpaka mtsogolo, chimene iye anachita, ndipo inu muwone momwe mungayendetsere mpingo.

Tsopano ife tikupeza, kuti, apo Iye anazindikiritsidwa kwa Simoni.

109 Ndiye ife tikumuwona iye, Nataniele, ife timubweretsa iye pamenepo. Ndipo Nataniele anati, "Tsopano, dikira miniti. Tsopano, iwe ukuyenera kuti ukulakwitsa."

110 "Ayi, sindikulakwitsa. Iwe ukumudziwa nsodzi wachikulire uja amene ife tinkakonda kuwedza naye kumusi uko?"

"Inde."

"Ukudziwa kuti sankatha kulemba dzina lake."

"Uko nkulondola, pa lisiti limenelo, la nsomba nthawi imeneyo."

111 "Pamene iye anayenda kupita mu Kukhalapo kwa Uyu amene ine ndikumudziwa kuti ndi Mesiya . . . Tsopano, ine ndikufuna ndikufunse iwe, Nataniele. Ndiwe wophunzira wabwino, m'Hebri wabwino, komanso wowerenga wabwino wa Baibulo. Mesiya adzakhala chiyani pamene Iye adzabwera?"

"Chabwino, Iye adzakhala mneneri, chifukwa Baibulo linati Iye . . . "

112 "Chabwino, iwe unganene chiyani ngati ine nditakuuza iwe kuti Iye anamuuza mwamuna uja, Simoni, yemwe iye anali, ndi yemwe ake, yemwe bambo ake anali?"

"Oh, ine sindingakhulupirire zimenezo."

"Chabwino, tiyeni tipite tikafufuze. Tiyeni tipite. Bwera udzawone." Mukuona?

"Kodi chiripo chirichonse chabwino chingachokere ku Nazarete?" iye anatero.

113 Iye anati, "Bwera udzawone." Limenelo ndi funso labwino. Osakhala kunyumba ndi kumazitsutsa Izo. Bwera ndipo udzadziwonere, wekha. Iye anati, "Bwera, bweretsa Baibulo lako ndipo udzafufuze izo." Apa iye akubwera.

"Kodi chiripo chinthu chabwino chirichonse chingachokere ku Nazarete?"

Iye anati, "Bwera, udzawone."

114 Ndipo pamene iye anadzayenda kupita mu Kukhalapo kwa Yesu, Yesu anamuyang'ana iye. Tsopano Iye anati, "Taonani m'Israeli amene mwa iye mulibe chinyengo."

Iye anati, "Rabi, ndi liti limene Inu munayamba mwandidziwa ine?"

115 Iye anati, "Filipo asanakuyitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, ine ndinakuwona iwe."

116 Iye anati, "Rabi, Inu ndi Mwana wa Mulungu. Inu ndi Mfumu ya Israeli."

117 Chifukwa chiyani? Khalidwe Lake linamuzindikiritsa Iye. Chifukwa chiyani? Ahebri mutu wa 4, ndime ya 12, amanena kuti, "Mawu a Mulungu ndi amphamvu kwambiri, akuthwa kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, logawaniza pakati, ndipo ozindikira malingaliro ndi zokhumba za mtima."

118 Ndicho chimene aneneri ankachita, ndipo iwo anali Mawu. Iwo anali Mawu mu m'badwo wawo, koma apa panali chidzalo

cha Mawu. Mukuona? Iwo anali amene ankakhoza kuwauza iwo chimene chinachitika, kuzindikira malingaliro; ndi chimene chinali, ndi chimene chiri, ndi chimene chiri nkudza.

119 Kotero apo Iye anali atayima pamenepo. Oh, apo panali ena a iwo atayima pamenepo, anati . . . Iwo ankayenera kuti akapereke yankho kwa osonkhana awo. Iwo ankayenera kuti akachite zimenezo, chifukwa apo—ntchito zamphamvu zinachitidwa ndipo iwo sakanatha kuzikana izo.

120 Mwaona, iwo anali nawo kale machiritso, kunena za machiritso. Iwo anali ndi thamanda la Betsaida, kumtunda uko, inu mukudziwa. Iwo, Betsaida, iwo ankalowa mu thamanda limenelo ndipo ankachiritsidwa. Iwo amakhala ndi machiritso Auzimu mu m'badwo uliwonse, koma apa panali mneneri.

121 Iwo—iwo ankayenera kuti achite zimenezo. Inu mukudziwa chimene iwo ananena? "Munthu uyu ndi Belezebule, wam'bwebwe. Iye amachita . . . "

122 Yesu anati, "Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo. Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera mu m'badwo winawo, kuti udzachite Mawu omwewo, liwu limodzi . . . liwu limodzi lotsutsa Izo, silidzakhululukidwa konse, osati mu dziko lino kapena mu dziko limene likubwera." Kumeneko ndi kuchitira mwano, kuwutcha Mzimu wa Mulungu kuti mzimu wonyansa, umene ukuchita ntchito ya Mulungu. Muganizire zimenezo mwamphamvu kwenikweni tsopano. Kumbukirani, muzisunge izo mmalingaliro anu.

123 Inde, umo ndi momwe Iye anazindikiritsidwira dzulo. Ameneyo anali Yesu, dzulo. Ndipo ngati Iye ali yemweyo lero, Iye angachite chomwecho. Umo ndi momwe Iye anadzizindikiritsira Yekha ngati Mesiya. Umo ndi momwe iwo anamudziwira Iye, mwa ntchito imeneyo. Onani, izo ndi . . .

124 Pali mitundu itatu yokha, mitundu itatu ya anthu, ndiyo, Myuda, Wamitundu, ndi Msamariya. Ndipo iwo ndi—anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Tsopano, ngati ife timalikhulupirira Baibulo, iwo onse anachokera kwa ana a Nowa, ndipo awo ndi Myuda, Wamitundu, ndi Msamariya.

125 Tsopano, Wamitundu sankayembekezera Msama- . . . Mesiya. Ife tinali ndi chibonga pa nsana pathu, ndipo tinkapembedza mulungu wachikunja. Ife achi Anglo-Saxon, ndi ena otero, mmasiku amenewo, ife tinali achikunja, Aroma ndi Agriki, ndi ena otero. Ife sitinkayembekezera Mesiya ayi. Koma Ahebri ankayembekezera zimenezo, ndipo Iye . . .

126 Kumbukirani, mumvetsetse izi mwatcheru tsopano. Iye amangowonekera kwa iwo amene akumuyembekezera Iye. Amangowonekera kwa iwo amene akumuyembekezera Iye. Amadzizindikiritsa Yekha kwa iwo amene akumuyembekezera Iye.

127 Ndipo Iye amazidzindikiritsa Yekha kwa Ayuda, nthawi zambiri. Tikafika mkati mwa sabatayi, titenga anthu owonjezera. Koma pakali pano . . .

128 Tsopano panali Asamariya, iwo ankamuyembekezera Iye, nawonso. Kotero Iye anali pa ulendo Wake waku Yeriko, kotero Iye ankayenera kudutsira njira ya ku Samariya, ndipo Iye anafika ku mzinda wa Sukari. Pafupifupi leveni koloko, kapena thwelovu, ndipo Iye anawatumiza ophunzirawo mu mzinda, kuti akapeze zakudya zina.

129 Pamene iwo anali atapita, mkazi wa mbiri yoipa wa mu mzindawo anatulukira, mwinamwake mtsikana wokongola. Iye mwinamwake anali, inu mukudziwa, anali atakanidwa ndi makolo ake ndi chirichonse, ndipo iye anali asanawone kalikonse mu tchalitchi, kotero iye ankangopeza thandizo lake mwa njira yoyipa, pokhala ndi amuna ambiri. Ndipo iye anabwera pa chitsimepo, ndipo apo panali Yesu atakhala pamenepo, Myuda.

130 Iye mwinamwake ankawoneka wokulirapo pang'ono kuposa chimene Iye anali kwenikweni, chifukwa Iye anali ndi zaka sarte zokha, ndipo ife tikupeza mu Yohane Woyera 6 kuti iwo ankanena kuti Iye ankawoneka ngati Iye anali ndi zaka fifite. Iwo anati, "Iwe sunapitirire zaka fifite, ndipo ukuti unamuwona Abrahamu?"

131 Iye anati, "Abrahamu asanakhalepo, Ine ndine." Mukuona? Koma mwina, ntchito Yake, ikhoza kukhala kuti inayika kupsyinjika kwakukulu pa Iye.

132 Apo Iye anali, atakhala moyang'anizana ndi khoma, ndipo mkazi uyu anabwerapo ndipo anatenga chaching'ono . . . Inu amene muli, kumusi kuno Kummwera, chotungira, inu mukudziwa, ndi chokolera. Kudakali zitsime zazing'ono zakalezo kumeneko, ndipo mwanjira yomweyo. Ndipo panali powonekera papang'ono, monga choncho. Ndipo—ndipo iye anatsitsira mtsuko uwu pansi.

133 Inu mukuyenera kuwawona akazi amenewo. Akazi inu mumayankhula za kuyenda moyenera! Ine ndawawonapo iwo akutenga mitsuko imeneyo, imene mmalowa pafupifupi magaloni faivi, ndipo iwo amayitenga ndi kuyisenza iyo pamitu pawo, umodzi pamwamba apo. Kuyika umodzi mchiuno chimodzi, ndi wina mbali yinayo, ndi kumayenda, akuyankhulana wina ndi mzake, ndipo osataya dontho limodzi. Kumangoyenda mwabwino basi monga momwe inu munayamba mwawonapo.

134 Tsopano Kummawa, mwaona, akazi oyipa ndi akazi abwino samayanjana pamodzi. Ndi zosiyana ndi kuno, koma—koma iwo sangakhoze kumeneko. Iye amayikidwa chizindikiro, amayikidwa chizindikiro. Ndizo zonse. Ngati iye akhala konse ndi mwamuna wolakwika, iye samayanjananso nawo. Koma

kumeneko. . . Izo zonse zinasokonezeka kuno tsopano, ife timazipeza chomwecho, koma uko sizimatero.

135 Kotero iye samatha kubwera ndi anamwali, mmawa. Iye ankayenera kuti abwere pafupifupi masana, kuti adzatunge madzi, ake.

136 Kotero iye anayamba kutsitsa mtsukowo. Koma munali mbewu yokonzedweratu mwa mkazi wamng'onoyo. Iye anayika pansi mtsuko wamadziwo, ndipo iye anamumva Mwamuna akuti, "Ndipatse Ine akumwa. Ndibweretsere Ine akumwa."

137 Iye anatembenuka ndipo anayang'ana mozungulira, iye anamuwona Myuda uyu. Ndipo Myuda uyu, mwinamwake, Mwamuna wa usinkhu wapakati. Sindikudziwa chimene chinali m'malingaliro ake pamenepo. Kotero iye anati, "Bwanji, si chamwambo kwa Inu, pokhala Myuda, ndi kundipempha ine, mkazi waku Samariya." Mwaona, iye sankadziwa chimene icho—chimene icho chinali. Iye basi. . . mwinamwake mwamunayo mwinamwake ankayamba kuchenjera ndi iye, kotero iye. . . Anati, "Si chamwambo kwa inu Ayuda."

138 Ndipo kotero zokambiranazo zinapitirira. Kodi Iye ankayesera kuti achite chiyani? Iye ankayesera kuti akope tcheru chake. Atate anali atamutumiza Iye kumtunda uko, koma tsopano Iye ankayenera kuti apeze chifukwa chomwe anapitira kumeneko.

139 Iwo ankayembekezera Mesiya. Iye anali atadzizindikiritsa Yekha ndi Ayuda, tsopano apa Iye ali ndi—ndi—ndi Asamariya.

140 Ndipo anati, "Si chamwambo kuti inu mu—mu—mundifunse ine, mkazi waku Samariya, zoterozo."

141 Kotero Iye anati, "Koma ngati iwe ukanadziwa Amene ukuyankhulana naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa. Ine ndikanakupatsa iwe madzi amene sukanabweranso kuno kudzatunga."

142 Ndipo iwo anayamba kuyankhulana za kupembedza. Molunjika Iye anapeza lomwe vuto lake linali. Ife tonse tikudziwa chimene ilo linali, amuna ochuluka kwambiri. Iye anamuyang'ana iye, anati, "Mkazi, pita ukatenge mwamuna wako ndipo ubwere naye kuno."

Iye anati, "Ine ndiribe mwamuna aliyense."

143 Iye anati, "Iwe wanena zoona, pakuti iwe wakhala nawo faivi, ndipo amene ukukhala naye tsopano si wako."

144 Muwoneni mkazi ameneyo. Tayang'anani pa kusiyanako pakati pa iye ndi bungwe lija. Mumuwone iye ngati munthu payekha. Awoneni Afarisi amenewo, anati, "Munthu uyu ndi Belezebule." Tayang'anani pa mkaziyo. Osati iye.

145 Iye anatembenuka, ndipo iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri." Ah, apo pali Kuwala

kumeneko, mwaona. Pamene Mwana amenya Mbewuyo, ndipo mtundu woyenera, iyo idzabala Moyo, motsimikiza basi monga dziko. Anaikhudza Mbewu imeneyo mu mtima wa hule wamng'ono ameneyo! Iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Tsopano, ife tikudziwa kuti ndi zimenezo, ife takhala kwa zaka mahandirede kuchokera pamene ife tinali ndi mneneri, ndipo ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, ife tikumuyembekezera Iye, ndipo pamene Mesiya adzabwera, ichi ndi chinthu chimene Iye ati adzachite."

146 Ndi chimenecho chizindikiro cha Mesiya. Kodi inu simukuwona? Anali Mesiya amene anali mwa Mose. Anali Mesiya amene anali mwa Enoki. Anali Mesiya mu m'badwo uliwonse. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndi Khristu nthawi zonsezo.

147 Anati, "Ine ndikudziwa. Ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, icho ndi chimene Iye ati adzachite."

Iye anati, "Ine ndine Iye amene ndikuyankhula ndi iwe." Oh, mai!

148 Pakumva zimenezo, iye anagwetsa mtsukowo, anathamangira mu mzindawo, ndipo anati, "Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wandiuza ine zomwe ine ndinazichita. Kodi uyu si Mesiya yemweyo?"

149 Ndipo anthu a mzinda umenewo, popanda kuziwona izo zikuchitidwa, mzinda wonse unakhulupirira pa Iye. Uko nkulondola. Chifukwa chiyani? Khalidwe Lake la chimene Iye anali. Iye anazindikiritsidwa ku mzinda umenewo wa Sukari. Iye anazindikiritsidwa, Mesiya wa Mulungu, mwa khalidwe Lake, khalidwe lomwe linali mwa Iye. Chifukwa, Iye anali—Iye anali Mulungu wa aneneri. Iye anali Mneneriyo. Iye anali Mneneri akuwonetseredwa. Iye nthawizonse wakhala ali, kutsika kudutsa mu m'badwo, yemweyo, ndipo ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

Tsopano kuti tifulumire ndi kutseka.

150 Ife timauzidwa, mu Zakariya 14:6 ndi 7, kuti, "Lidzafika tsiku," mneneri ananenera, "limene iwo sangalitche usana kapena usiku." Ndi tsiku lolunda, lachimbuuzi, lakuda, "koma mu nthawi ya kumadzulo kudzakhala Kuwala." Baibulo linanena chomwecho.

Tsopano penyani, potseka.

151 Mwamalo, dzuwa limatuluka pa anthu a Kummawa, poyamba. Ilo limatulukira Kum'mawa ndipo limakalowa Kumadzulo. Tsopano nditsatireni ine mwatcheru. Chitukuko chayenda limodzi ndi dzuwa. Ife tonse tikudziwa zimenezo, sichoncho ife?

152 Chomwechonso watero Uthenga. Uthenga unayambira Kummawa. Iwo unachokera Kummawa; unadzawoloka, mpaka

ku Germany, kudutsa Mediterranean, kukalowa mu Germany; kuchokera ku Germany, kudutsa English Channel, kupita ku England; kuchokera kumeneko, kuwoloka Atlantic, mpaka ku United States, ku Gombe la Kummawa; ndipo wayenda kupita ku Gombe la Kumadzulo. Tsopano Kummawa ndi Kumadzulo kwakumana.

153 Ndipo dzuwa lomwelo lomwe limatuluka Kummawa, ndi dzuwa lomwelo lomwe limalowera Kumadzulo.

154 Tsopano penyani. Mwana, M-w-a-n-a, anatuluka ngati Mesiya, pa anthu Akummawa.

155 Ndipo tsopano ife takhala ndi tsiku, chichokereni Iye, la zipembedzo ndi kukhala pamodzi, ndi—ndi zina zotero. Ife takhala nako kuwala kokwanira monga tsiku lolunda pamene dzuwa labisika ndi mitambo. Ndipo iwo akhala nazo zipembedzo. Ife tinamanga zipatala. Ife tinamanga masukulu. Ife tamanga mabungwe. Ife tachita zinthu zonsezi chimodzimodzi basi momwe ife tikuyenera kumachitira izo.

156 Koma Iye anati, "Mu nthawi ya kumadzulo kudzakhala Kuwala." Yesu yemweyo, mu mphamvu Yake ya chiwukitsiro, adzawukanso, monga Iye analonjezera mu Malaki 4, monga Iye analonjezera mu Yohane Woyera 14:12. Monga Iye analonjezera mu Luka 17. "Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu."

157 Taonani chimene chinachitika mmasiku a Sodomu. Abrahamu, mmodzi yemwe anali ndi lonjezo la mwana wakudzayo, apa ife tikumupeza iye kumusi uko, ndipo ife tikuwona chizindikiro chimene chinachitidwa.

158 Kumusi uko mu Sodomu, ife tinawona chimene chinachitika. Ndipo inu mukudziwa kuti ife sitinayambepo...Tsopano, kumeneko, Loti anali choyimira cha mpingo wathupi, uko mu Sodomu, bungwelo, ndipo iwo ali ndi mtumiki kumusi uko. Apo panali atumiki angapo amene anapita kumeneko, Billy Graham wamakono ndi Oral Roberts. Ndipo kodi inu mukudziwa chiyani? Sipanayambe pakhalapo nthawi, mu mbiriyakale ya mpingo, imene munthu anayamba watumizidwapo kwa mpingo ku dziko lonse, wokhala ndi dzina lake lothera ndi h-a-m, mpaka nthawi ino. Billy G-r-a-h-a-m, zilembo sikisi. A-b-r-a-h-a-m ndi zilembo seveni. Koma Billy G-r-a-h-a-m ali kunja uko mu Sodomu, akumenya kumeneko ndi kuwayitanira iwo atuluke.

159 Koma, kumbukirani, panali Mmodzi amene anali ku mpingo wauzimu, yemwe anali kumeneko, Abraham woyitanidwa-atuluke. Penyani mtundu wa chizindikiro chimene Iye anapereka. Iye sanalalikire zambiri za Uthenga, Iye anangowauza iwo za malonjezo amene anali pafupi kuchitika . . . Ndipo Iye anati, "Alikuti Sarah?" Tsopano, kumbukirani, iye anali Sarai dzulo lake izo zisanachitike, ndipo iye anali Abram

dzulo lake izo zisanachitike. Tsopano Iye anati, “Abraham, A-b-r-a-h-a-m, ali kuti S-a-r-a-h?” osati S-a-r-r-a. “Ali kuti *Sarah*, ‘mwana wamkazi wa mfumu,’ mkazi wako, atate wa mafuko?”

Anati, “Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu.”

160 Ndipo Iye anati, “Ine ndidzakuchezerani inu molingana ndi nthawi ya moyo.”

161 Munthu amene anadya mnofu wa ng’ombe, kumwa mkaka wa ng’ombe, ndi kudya makeke a chimanga, kumwa mkaka. Mwamuna, fumbi liri pa zovala Zake, ndipo atakhala pamenepo atatembenuzira nsana Wake ku hema. Anati, “Ali kuti Sarah mkazi wako?”

Anati, “Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu.”

162 Ndipo Sarah anati, “Ine, mkazi wokalamba momwe ndiririmu, zaka handirede, monga mwamuna ndi mkazi tinasiya kalekale. . .zokhala ndi chisangalalo ndi mbuye wanga, ndipo iye wokalamba, nayenso?” Baibulo linati “okalamba kwambiri,” zinakhala zaka ndi zaka. Iye anali atadutsa kusintha kwa thupi kwa zaka forte-faivi, kapena kupitirira apo, mwinamwake zaka fifite-faivi atadutsa kusintha kwa thupi. “Ndipo ine kudzakhala ndi chisangalalo ndi mwamuna wanga, monga mkazi wamng’ono?” Iye anaseka mwachinunu, inu mukudziwa.

163 Ndipo, uja, Mwamuna uja, Mwamuna uja anali mu mnofu waumunthu uja, anati, “N’chifukwa chiyani Sarah anaseka?”

164 Chinachitika ndi chiyani? Abraham anamutcha Munthu ameneyo, “Elohim,” Mulungu Wamphamvuzonse akuyimiridwa mwa munthu.

165 Yesu Ambuye wathu anati, “Monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala pa Kudza,” ndipo penyani, “pamene Mwana wa munthu akuwonetseredwa, kudziwitsidwa,” Luka 17. “Pamene Mwana wa munthu, mmasiku otsiriza, akuwululidwa. Mwana wa munthu akuwululidwa, Uthenga Wake ukumuzindikiritsa Iye monga zinali mmasiku a Loti.”

166 Taonani momwe iwo akuchitira tsopano, mafuko opotozedwa. Oh, mai! Tayang’anani pa amuna ogonana, ndipo tayang’anani pa zomwe ife tiri nazo tsopano. Mpingo uli mu nyansi. Fuko liri mu nyansi, ndi chinthu chonsecho. Mulungu akugeya izo, kuchokera pamwamba, pansi pa dziko lapansi. Chinthu chonsecho ndi nyansi.

167 Mwapamalo, komanso mu zogwirika, zochitikazo zakhazikitsidwa. Kodi iyi si nthawi yoti Mulungu abwererenso mu thupi la munthu, “Mawu amene ali akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo ozindikira malingaliro ndi zolinga za mu mtima,” kuti awonekere pa chochitika, kuti amupange Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Ndi Mawu olonjezedwa amene anayikidwa ku tsiku lino. Ife

tikukhala moyo mu tsiku lino, ndipo Mulungu ali pano ndi ife, kuti adzawonetsere izo ndi kudzazipanga izo kukhala zoona.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

168 Atate Akumwamba, Inu munati, "Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo." Ife tikukuwonani Inu, Ambuye, mwa zizindikiro zonse; mafuko akusweka; Israeli ali mu dziko lakwawo; zivomezi m'malo osiyanasiyana; mitima ya anthu ikulephera; malingaliro opotozedwa; otayika pa Choonadi. "Monga Yambre ndi Yane anapikisana ndi Mose," Inu munati, "anthu amalingaliro opotoka, operekedwa ku zinyengo, kuti akhulupirire bodza ndi kuweruzidwa nalo ilo." Koma Inu munalonjeza, mu tsiku limenelo, kuti Inu mukanadzadzizindikiritsa Nokha, Mwana wa munthu akanadzawululidwa, Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, mwa khalidwe Lake lomwelo limene linamuzindikiritsa Iye mu m'badwo uliwonse.

169 Mulole Iye, usikuuno, Ambuye Mulungu, Yehova wamkulu, Elohim, atsikire mwa anthu Anu, usikuuno, Ambuye. Tsikani ndipo mudzadzizindikiritse Nokha, kuti okhulupirira akhoze kukhulupirira. Kuti anthu akhoze kumvetsa ndi kudziwa kuti Inu mukadali Mulungu, ndipo Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndiyeno, Ambuye, iwo amene anadzozedweratu ku machiritso, ndi iwo amene anadzozedweratu ku Moyo Wamuyaya, afikire ndi kuwagwira, Ambuye, pakuti ino ndi nthawi ya kuchezeredwa. Mulole kuti izo zisadutse pachabe. Ine ndikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

170 Ndi angati akukhulupirira kuti izo ndi zoona, umenewo ndi Uthenga? Tsopano kodi ife tikukhala mu tsiku limenelo? Icho ndi chinthu chotsatira. Ngati izo ziri, Mulungu ali wokakamizika kuti azizindikiritse izo.

171 Tsopano ngati inu mungandipatse ine tcheru chanu chosagawanika. Ine ndingochedwa pang'ono chabe, ine ndinakuuzani inu usikuuno, mwinamwake maminiti fifitini.

172 Ife tinapereka makadi apemphero...ma A, ma A. Chabwino, tiyeni tiyambe mofulumira. A, nambala wani. Ine ndidzikuyitanani inu mmodzi pa nthawi, kotero kuti inu muzikhoza kuyima cha apa, ngati inu mungathe. A, nambala wani. Ndani ali ndi khadi la pemphero A, nambala wani, kwezani mmwamba dzanja lanu? Tsopano ngati inu simungathe kukweza mmwamba, ine ndi...ena a iwo abwera kudzakutengani inu. A, nambala wani, chabwino. Tsopano muzingobwera pamene inu mukuitanidwa, nambala yanu yokha. Chabwino, A, nambala wani. Chabwino.

173 Nambala thuu, kodi mungakweze mmwamba dzanja lanu? Nambala thuu, khadi la pemphero A, nambala thuu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Kodi inu mungabwere, dona? Tsopano

ngati pali wina wolumala ndipo sangathe kudzuka, othandizira adzakunyamulani inu. Nambala thuu.

174 Firii, mungokweza dzanja lanu. Zisungani nthawi, mwachangu kwambiri, ngati mungayitane . . . Nambala firii, kodi mungakweze dzanja lanu? Pomwe pano, dona. Nambala foro, kwezani dzanja lanu, nambala foro. Pemphero . . . Nambala foro, bwerani. Chabwino. Nambala faivi, khadi la pemphero nambala faivi. Pomwe pano, dona. Nambala sikisi.

175 Huh? Kodi iye angathe kuyenda? Chabwino. Izo ndi . . . Kapena, mumutengere iye mpando pamusi apo. Donayo akudwala, ine ndikuganiza, kapena mwinamwake mwamuna wake, aliyense amene anakhala ndi iye pamenepo. Kapena ndi . . . Mutengereni iye mpando pamenepo, iye ali . . . Chabwino.

176 Nambala seveni. Nambala eyiti. Nambala naini, naini. Ine ndikumva . . . Eya, apa, naini, naini. Teni, nambala teni, khadi la pemphero teni? Leveni, thwelovu, sartini, sartini, fortini. Pitani pansi mpaka kumathero enawo pamusi apo, fortini. Fifitini. Chabwino, pitani—pitani kumbuyo kwa iwo komwe.

177 Tsopano mungodikira miniti yokha mpaka awa alowe mu mzere, tiwone pamene ife tiri pano miniti yokha. Tsopano nonse a inu mungogwira khadi lanu miniti yokha.

178 Tsopano ndi angati mu msonkhano uno amene a—akudwala, ndipo alibe khadi la pemphero? Kwezani mmwamba manja anu monga *chonchi*. Chabwino. Aliyense . . . Ine sindikusamala pamene inu muli. Chabwino.

179 Tsopano mungokhala molemekeza. Tsopano, penyani, pamene iwo akukonza mzere wa pempherowo, inu nonse mundipatse ine tcheru chanu chosagawanika tsopano. Inu mukuyenera muzimvetsera ku zimene ine ndizikuuzani inu. Mukuona? Zindikirani.

180 Nthawi ina kunali mkazi, Yesu ankadutsa mu dzikolo ndipo Iye anawoloka nyanja, ndipo Iye anapita ku malo ndipo uko kunali mkazi amene anali ndi vuto la magazi. Ndipo ansembe onse ndi iwo anali kumeneko, iwo anali akumutonza Iye, ndithudi. Ndipo panali gulu kunja uko limene linkamukhulupirira Iye. Ndipo Iye ankadutsa mu khamulo. Ndipo mkaziyo anati mumtima mwake . . .

181 Tsopano mvetserani mwatcheru tsopano. Kodi inu mukumvetsera? Nenani, "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Uyu, tsopano, mkaziyu . . . Mwaona, pa chirichonse, zikusokoneza zimene inu mukuchita, inu mukuona. Munthu aliyense ndi a . . . Sindikuchita nanu ngati a—ngati thupi. Ndikuchita nanu ngati mzimu, solo. Mukuona? Ndipo kusuntha kumeneko, inu mukuika malingaliro anu kumapita kwinakwake, mwaona, ine ndikuyesetsa kuti ndigwire zimenezo. Zindikirani tsopano, panali mwamuna amene anayang'ana pa Paulo, akukhulupirira moonamtima;

Paulo anati, "Ine ndikuwona kuti muli ndi chikhulupiriro kuti muchiritsidwe." Mukuona? Tsopano zindikirani.

182 Mkazi uyu, pamene iye amadutsa apa, iye amalephera kufikira kwa Iye. Aliyense ankayika manja awo momukumbatira Iye, chirichonse. Tiyeni tinene kuti, kungoyerekeza—kungoyerekeza tsopano, iye analibe khadi la pemphero ndipo iye samakhoza kulowa mu mzere.

183 Ndipo kotero, aliyense, "Moni, Rabbi! Ndikuti, Kodi Inu ndi mneneri? Ife—ife timakhulupirira kuti akudza mneneri, koma ine—ine sindikudziwa panobe. Mwaona, ine—ine sindikutsimikiza. Ine ndichotsedwa mu mpingo wanga ngati ine ndingakhulupirire Zimenezo." Mukuona? Ndipo, inu mukudziwa, nkhani yakale yomweyo kumangobwereza.

184 Kotero ndiye mkazi wamng'ono uyu, iye anakhulupirira izo. Kotero iye anazembera, ndipo anati, "Ngati ine ndingakhoze kukhudza mphonje ya chovala Chake, ine ndichiritsidwa." Kotero iye anamukhudza Iye.

185 Tsopano ngati alipo aliyense amene anayamba wawonapo chovala chaku Palestina, iwe umakhala ndi chovala chamkati, ndipo kenako chovala chakunja chimalendewera momasuka. Tsopano, ngati mkazi wina akanakhudza chimodzi cha chikhotho cha amuna inu, mchira chabe wa chikhotho chanu, monga *choncho*, ndi kuchokapo, inu simukanadziwa izo nkomwe mu unyinji woterowo. Nanga bwanji chovala chachikulu chija chomwe chinkalendewera kutalikirana *chomwecho* ndi Iye? Ndipo iye anali pansi pa mawondo ake ndipo anangokhudza chovala Chake, ndipo anabwerera.

Yesu anayima. Iye anati, "Ndani wandikhudza Ine?"

186 Ndipo penyani chimene Petro ananena, tsopano, ali ndi makiyi aku Ufumu. Mwakuyankhula kwina, tiyeni tingoziyika izo m'mawu athu amasiku ano, "Bwanji, Ambuye, Inu mukunena zina za zinthu zoipa kwambiri! Chabwino, anthu amenewo aganiza kuti Ndinu wopenga, pali chinachake cholakwika. Aliyense wakukhudzani Inu."

187 Aliyense anati, "Moni, Rabbi! Akuti, kodi Ndinu mchiritsi Wauzimu? Kumanena chomwecho. Inu mukuti. . . Dikirani, ine ndiri ndi manda odzaza anthu kuno, ngati Inu mukufuna kutidzutsira ife mmodzi. Bwerani kuno, ndipo ife tikukhulupirirani Inu ngati Inu mungachite zimenezo." Ndipo basi ena anali a Iye ndi ena akumutsutsa, chimodzimodzi basi monga momwe zimakhalira mu unyinji uliwonse, mwaona; ndi kumasereula, ndipo ena akumukhulupirira Iye.

188 Ndipo Petro anati, "Bwanji, aliyense akukukhudzani Inu! Inu munganene bwanji chinthu choterocho monga icho?"

189 Iye anati, "Koma ndazindikira kuti ndafooka; ukoma wachoka mwa Ine," imeneyo ndi mphamvu.

190 Penyani, Iye anayang'ana mozungulira pa omvetserawo ndipo Iye anamupeza mkazi wamng'onoyo. Iye sakanakhoza kubisa izo. Mukuona? Iye anali ndi Mbewu imeneyo ili mmenemo. O Mulungu, tipatseni ife Mbewu imeneyo! Ndicho chimene ife tikuchisowa pakali pano. Iye anamupeza iye, ndipo Iye anamuuza iye za vuto lake la magazi. Anati, "Chikhulupiriro chake chinali chitamuchiritsa iye."

191 Onani, inu mukuti, "Kuti, ngati Iye akanakhala pano usikuuno, ine ndikanachita chinthu chomwecho." Ngati Iye akanayenda kudutsa mchipinda chino, usikuuno, inu mukukhulupirira kuti ngati inu mukanamukhudza Iye inu mukanachiritsidwa?

192 Chabwino, ndiloleni ine ndikuuzeni inu. Mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 3, ilo limanena kuti, "Pakali pano Iye ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu." Ndi angati akukhulupirira zimenezo kuti ndi Choonadi? Mukuona? Chabwino, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kodi Iye angachite motani lero? Chimodzimodzi monga Iye anachitira dzulo. Nkulondola uko?

193 Tsopano simukusowa kuti muchite kudzakhala pano. Inu mungokhulupirira, ndipo inu munene izi, "Tsopano, Ambuye, ine—ine. . . Zonsezi ndi zachilendo, koma mwamunayo akunena izo kuchokera mu Baibulo. Izo zikumveka. . . " Izo zinkamveka mwachilendo mu m'badwo uliwonse. Koma fufuzani izo, ndipo muwone ngati Malemba. . .

Yesu anati, "Fufuzani Malemba; Iwo akuchitira umboni za Ine." Mukuona?

194 Tsopano fufuzani Malemba. Izo ndi zoona. Ife tiri mmasiku otsiriza. Chirengedwe chonse chikutsimikizira kuti ndi masiku otsiriza. Mpingo mu chisokonezeko chake, inu nonse mukupita kokaphedwa kwakukulu kwachipembedzo posachedwa ndithu, cha kuno, inu mukuona, basi manthu wa hule ndi ana ake onse aakazi, monga momwe—monga momwe Baibulo linanenera, kutenga chilemba cha chirombo ndipo osadziwa izo. Mukuona? Oh, tifika ku zimenezo mtsogolo.

195 Zindikirani tsopano, Iye adakalipo, ngati ife tingapeze Kukhalapo Kwake pano. Inu kunja uko opanda khadi la pemphero, inu mukhudze chovala Chake. Iye ndi Wansembe Wamkulu. Kodi mumachita bwanji zimenezo? Ndi chikhulupiriro chanu? Khudzani chovala Chake ndi kuwona ngati Iye satembenuka ndi kudzachita chinthu chomwecho chimene Iye anachita nthawi imeneyo. Baibulo linati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Zimenezo zingakhale zokhutitsa kwambiri. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Chabwino.

196 Tsopano, aliyense, aliyense asagwedezeke tsopano. Khalani olemekeza kwenikweni. Mwaona, inu mukuyenera kulemekeza Mzimu Woyera. Kulemekeza! Njira yokhayo imene inu mutadzalandirire chirichonse kuchokera kwa Mulungu, ndi kulemekeza Uthenga Wake. Ulemekezeni Iwo. Tsopano mvetserani.

197 Tiyeni tingotenga, nonse inu Amethodisti, Abaptisti, Achipentekoste, ndi Akatolika, ndi nonse, mungotenga chipembedzo chanu, bungwe lanu, ndi kuliyika ilo cha apa, pambali, maminiti pang'ono, ndi kuti, "Ngati Iye ali Mawu, Mawu ndi ozindikira malingaliro amene ali mu mtima. Ameneyo anali Mesiya dzulo; ameneyo ndi Iye lero. Izo zikuyenera kukhala. Ndipo Iye analonjeza izo lero, tsopano."

198 Tsopano apa pali dona wamng'ono wayima apa. Tsopano aliyense asasunthe. Mungokhala molemekeza kwenikweni ndipo imani njii. Tsopano ine, mwa—mwa mphatso . . .

199 Tsopano, mphatso si chinachake chimene inu mumangochitenga ngati—nkhwangwa yodulira, ndi kupita kukadula ndi kucheka. Izo ndi zolakwika. Mphatso ndi kudziwa kudzichotsa wekha panjira. Ndi kungodzikhazikitsa wekha ndi kudzitulutsa wekha, ndipo kenako Mulungu amabwera mkati ndi kudzakugwiritsa iwe ntchito momwe Iye akufunira kuchitira. Mphatso ndi kuzichotsapo wekha panjira. Mukuona? Osati chinachake chimene iwe umachiyika mdzanja lako, nkumapita kumakabaya ndi kumakamata; ameneyo, ameneyo si Mulungu. Mukuona? Chinthu chimene ife timachita ndi kungodzichotsa tokha panjira, kenako Mzimu Woyera umabwera mkati ndipo umadzayamba kuigwiritsa ntchito iyo mwanjira iliyonse imene Iye akufuna kuti ayigwiritsire ntchito iyo.

200 Tsopano inu mumayenera kudzichotsapo nokha panjira. Ziribe kanthu chimene Mulungu angachite pano, Iye akuyenera kuti achichite icho pa inu, aponso. Ziribe kanthu momwe Iye angandidzozere ine, Iye akuyenera kuti akudzozeninso inu. Ngati Iye satero, "ntchito zamphamvu zambiri Iye sakanakhoza kuzichita."

201 Tsopano ine ndikukhulupirira kuti ndinamuwona winawake, mnyamata wamng'ono, amawoneka ngati, anakhala apa mu chikuku kapena chinachake. Ine ndimaganiza kuti ine ndinawona mwamuna kumbuyo uko. Ziribe kanthu chimene icho chiri, pamene inu mulipo, tsopano inu mungokhulupirira. Pano pali mkazi wamng'ono akuyenera kukhala apa, wawerama.

202 Tsopano kumbukirani, ine sindingathe kumuchiritsa aliyense. Palibe chinthu choterocho kuti munthu aliyense angachiritse. Ndi Mulungu. Ndi angati akumvetsa zimenezo tsopano? Machiritso anagulidwa kale. Ndi zoti zikupangitseni inu kukhulupirira kuti Kukhalapo Kwake kuli pano kuti

kusunge Mawu Ake. Tsopano ngati ine ndakuuzani inu Mawu Ake, kuti Iye analonjeza kuti akanadzachita izi, ndipo inu nonse mukukhulupirira izo; tsopano ngati Iye ati achite izo, izo zimuzindikiritsa Iye pano.

203 Tsopano apa pali mkazi wayima apa, dona wamng'ono. Iye ndi wamng'ono kwambiri kuposa ine. Ndipo apa pali chithunzi cha Yohane Woyera 4, mwamuna ndi mkazi akukumana nthawi yoyamba. Ndife alendo, ine ndikuganiza, dona wamng'ono, (kodi ndi choncho?) kwa wina ndi mzake. [Mlongoyo akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi]. Ife tiri. Tsopano ndikufuna kuti omvetsera ayang'ane. Ine sindikumudziwa iye. Ine sindinamuwonepo iye. Inu mwamumva iye akungonena izo. Ine sindikumudziwa iye. Iye sakundidziwa ine. Apa ife tayima.

204 Tsopano iye akhoza kukhala kuti akudwala. Akhoza kukhala ndi zachuma. Ilo likhoza kukhala vuto lapakhomo. Izo zikhoza kukhala za winawake. Ine—ine ndilibe lingaliro laling'ono kwambiri la izo. Ine sindikumudziwa mkaziyu, sindinamuwonepo iye.

205 Koma ngati Khristu akanayima pano, atavala suti iyi, imene Iye anandipatsa ine, tsopano. . .Ndipo ngati mkaziyu akananena kuti akudwala, ngati iye akanati, "Ambuye, kodi Inu mungandichize ine?" Bwanji, Iye anganene mobwereza, nayenso, Iye sangathe kuchitanso, ndipo akanamuuza iye kuti Iye anachita kale izo. Ndi angati akukhulupirira zimenezo? Mukuona? Iye sakanakhoza kuchita. . .

206 Koma Iye akanakhoza kudzizindikiritsa Yekha kukhala Mesiya. Iye akanadziwa zimenezo, chifukwa Iye akanazichita zimenezo, akanakhala ndi khalidwe lomwelo. Tsopano sindikanakhala ine ngati Iye akanachita zimenezo, chifukwa. . .

207 Poyamba, anali Mulungu mu Lawi la Moto, Mulungu pamwamba pathu; kenako Mulungu ndi ife, mwa Khristu; tsopano Mulungu mwa ife, mwaona, ana a Mulungu, mu kukhazikitsidwa kumene Khristu anabwera kudzachita, kudzawombola zikhumbo za Mulungu monga Iye anachitira pachiyambi.

208 Tsopano ngati Mawu Ake akukhala *muno*, ndipo ine ndanena Choonadi, ndipo ndi chimenecho, ndipo Mawu ali muno, mu mtima mwanga, ndiye Mulungu adzizindikiritsa Yekha monga icho kukhala Choonadi. Ndiye kodi izo zikuyenera kuchita chiyani kwa osonkhana awa? Kodi zikuyenera kuchita chiyani, pamene inu mukuliwona Lemba pomwe pano pamaso panu?

209 Tsopano, tsopano ine ndikuyenera kuti ndiyankhule ndi mkaziyu, chifukwa ine ndakhala ndikulalikira. Ndingoyankhula ndi iye miniti yokha, mpaka Mzimu Woyera uyambe kusuntha, ndiyeno inu nonse muyambe kukhulupirira. Tsopano, ndipo ife tidzakuwonani inu mawa usiku, tsopano. Mwaona, izi apa,

ndinu—inu muli m'dziko lina, dela lina, inu basi . . . simukudziwa chimene chikuchitika. Inu, aliyense amene ali pa maikrofoni, mungoyikweza iyo.

210 Tsopano ine ndikungofuna kuti ndiyankhule kwa inu monga Ambuye wathu anachitira ndi mkazi pa chitsime. Tsopano, ine ndi mwamuna, ndipo inu ndi mkazi, nthawi yoyamba imene ife takomana padziko lapansi. Ndipo—ndipo tsopano ngati . . . Iye anamuuza iye, "Ndikufuna madzi akumwa," kapena chinachake chonga icho. Inu mukuyikumbukira nkhaniyo? Kodi inu munayamba mwawerengapo zimenezo mu Baibulo? Inu munawerengapo izo? Chabwino.

211 Tsopano ngati Ambuye Yesu angachite chinthu chomwecho usikuuno, atakhala ngati akuwulula kwa ine chimene vuto lanu liri, kapena zomwe mwachita, kapena—kapena zomwe mwabwerera pano, kapena chinachake chonga icho, inu mungadziwe kuti icho—icho chiyenera kuti chikubwera kuchokera ku mphamvu ina ya chauzimu. Kodi mungakhulupirire izo kuti ndi zomwe ine ndakuwonetsani inu kuti Lemba limanena kuti izo zikanadzachitika? Tikuwona zivomezi, tikuwona dziko mu chisokonezo ichi, tikuwona zipembedzo momwe zirili, ndipo ndi nthawi yoti izo zichitike. Sichoncho izo? Inu mukukhulupirira zimenezo? Chabwino, tsopano, ngati Iye angadzizindikiritse Yekha ndi zimenezo, uyo angayenere kukhala Mulungu. Sindingakhale ine ngati munthu. Ine ndi m'bale wanu chabe.

212 Tsopano, inu ndi Mkhristu. Osati chifukwa chakuti inu mukuti, "alemekezeke Ambuye." Inu mukanakhoza kukhala wachinyengo mutayima pamenepo, mukunena zimenezo. Mukuona? Koma, ngati izo zinali, Iye akana—Iye akana—Iye akanadziwa izo. Mukuona? Koma ndikuwumverera mzimu wanu ukunjenjemera. Izo ndi zoona. Inu ndi Mkhristu.

213 Tsopano, ngati Ambuye Yesu ati awulule kwa ine chimene chavuta ndi mkaziyu, ndi angati ati akhulupirire tsopano ndi mtima wanu wonse?

214 Tsopano ndiyang'aneni ine, mlongo, mphindi yokha. Apa Izo zikubwera. Mwaona, tsopano ine basi . . . Iwo akuyenera kukhala masomphenya, mukuwona. Iwo akuyenera kuziwona izo mwanjira yina, chifukwa . . . Inde, bwana. Tsopano apa Izo ziri. Matamando akhale kwa Mulungu! Ine ndikuwutenga mzimu uliwonse, pansi pano tsopano, pansi pa ulamuliro wanga, mu Dzina la Yesu Khristu. Khalani olemekeza. Tayang'anani apa mphindi yokha, dona. Tayang'anani pa ine. Tsopano ndi nthawi yoti Ambuye anene chinachake kapena achite chinachake.

215 Ngati inu muli ndi kuzindikira, ngati inu munayamba mwachiwonapo chithunzi chija cha Kuwala kuja, Iko kwayima pakati pa ine ndi mkaziyo. Ndipo iye ali pano, iye akudwala matenda a magazi. Ndi matenda a shuga. Ngati izo ziri zowona,

kwezani mmwamba dzanja lanu. Mukuona? Tsopano bwanji ngati . . .

Winawake akhoza kunena kuti, “Inu mwangopeka zimenezo.”

216 Tayang’ana apa, dona wamng’ono. Ndinu munthu wabwino kwambiri tsopano. Tayang’ana kuno. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? [Mlongoyo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi]. Inu mukutero. Ine sindingathe kuchiritsa. Ndipo sindikudziwa chimene chakuwuzani inu. Chirichonse chimene chinali, chinali choona, sichoncho icho? Apa pali chinachakenso. Ine ndikuwona a—mtsikana. Ndi mtsikana wamng’ono amene inu mukumupempherera, amene ali ndi chinachake mu khutu lake. Ndi khutu lowukha, sikulondola kumeneko? Inde, inde, ndiko kulondola. Ilo likhala bwino. Inu mukhala bwino. Tsopano kazipitani, mukhulupirire zimenezo. Kazipitani, mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Mukhulupirire, mlongo.

217 Tsopano inu mukukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Ngati mutangokhulupirira, basi—mungokhala ndi chikhulupiriro. Mukuona? Musakayikire. Mwaona, “Iwo amazindikira maganizo ndi zolinga za mtima.” Ndi angati akudziwa kuti Mawu amachita zimenezo? Baibulo, zikusonyeza kuti mwakhala mukuwerenga Baibulo. Tsopano ziribe kanthu pomwe inu muli, mukhulupirire tsopano kudzozako.

218 Ndi angati anachiwonapo chithunzi chija cha Mngelo wa Ambuye, chimene chinajambulidwa kuno? Tsopano Kuwala komweko sikuli mapazi awiri kuchokera pamene ine ndayima pakali pano. Mwaona, izo ziri mu dera lina limene inu simungathe kuliwona. Ife timangokhala mu faivi; ili ndi lina. Tsopano mukhale molemekeza mphindi yokha.

219 Tsopano apa pali dona. Ine sindikumudziwa iye. Ine sindinamuwonepo iye. Ndife alendo kwa wina ndi mzake, ine ndikuganiza. [Mlongoyo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Ndipo iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukumana, ndipo basi mwamuna ndi mkazi. Ndipo ngati ine ndikanatha kuchita chirichonse kwa iwe, ine—ine ndithudi ndikanachita icho, koma ine—ine ndi munthu chabe.

220 Koma, mwa mphatso ya Mulungu, ine ndikufuna kuti ndizindikire, ine ndikufuna kuti Yesu adzizindikiritse Yekha ku Mawu amene ine ndangowalalikira kumene, kuti awonetsere kuti ili ndi oralo; Mawu amene anaperekedwa ku ora lino, kuti ife tadutsa mmalo achipembedzo, ife tikukonzekera kuti tipite mu Mkwatulo. Tikungoyesetsa kuwatengera anthu chikhulupiriro, kuti akhulupirire. Mukuona?

221 Chimodzimodzi monga mu—mapiramidi, mwaona, mwalawapamutu umenewo umene sunabwerepo konse. Pa

ndalama yanu ya dollar, iyo ili nayo. Mukuona? Tsopano utumiki umenewo ndi mwalawapamutu. Kumene izo zinali kumusi kuno mwa Luther, Wesley, ndi kumatsika mmusi, izo basi. . . Osati chiphunzitso cha piramidi tsopano, mwaona. Ine ndikungowonetsera ichi mwa kufotokozera. Mwalawapamutu umenewo udzayenera kukhala wangwiro kwambiri monga ina yonsewo, mpaka iwo utadzakwanirana molunjika mwa iyo. Utumiki wa Khristu udzakhala mu Mpingo Wake, ndendende basi monga Iye mu Mzimu, pamene Iye adzabwere kudzawutenga Mpingo, kuti adzawombole chinthu chonsecho, kenako nkumadzapita mmwamba.

222 Kodi iwe ukukhulupirira zimenezo? [Mlongoyo akuti, "Inde, ine ndikutero."—Mkonzi]. Ine ndinangonena zimenezo kuti ndimasuke pang'ono. Mwaona, ndizo, masomphenya ndi ovuta. Mkazi mmodzi uja anakhudza chovala Chake, ndipo Iye anati, "Ine ndamverera ukoma. . . " Ndipo ameneyo anali Mwana wa Mulungu. Nanga bwanji ine, wochimwa wopulu-. . . Mukuona? Iwe ukumvetsa? ["Inde."] Uh-huh. Tsopano ngati Ambuye Yesu ati awulule kwa ine mavuto ako, kodi iwe unga. . .?

223 Tsopano usachite mantha. Izo sizikupweteka iwe. Iwe uli ndi kumverera kwachirendo kwenikweni, iwe waona. Apo ndi pamene Kuwala kuja kunakhazikika pa iwe. Tsopano ngati izo, kotero kuti anthu adziwe, kweza dzanja lako mmwamba. Kotero iwe. . . Kumverera kokoma kwenikweni, kwabwino kwenikweni, mwaona, mwaona, kunangosunthira pa iwe. Tsopano iwe sungabise moyo wako nkomwe.

224 Iwe ukuvutika ndi vuto la chimfine. Ndipo izo nzoona. Uli ndi winawake pa mtima wako, amene iwe ukumupempherera. [Mlongoyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino, bwana, ameneyo ndi mwamuna wako. Ndipo mwamuna ameneyo ali ndi vuto ndi maso ake, limene linayamba chifukwa cha matenda a shuga. Ndipo izo nzoona. Mukuona? Chabwino. Tsopano, tsopano khulupirira ndi mtima wako wonse, awiri nonse a inu. Inu mukukhulupirira? Chabwino, bwana. Ndiye, molingana ndi chikhulupiriro chako, zikhale kwa iwe, mlongo wanga. Ambuye akudalitse iwe. Ukhale ndi chikhulupiriro. Osati ukayikire. Ukhulupirire ndi mtima wako wonse.

225 Tsopano ndife alendo, nafenso, kwa wina ndi mzake. Kodi iwe ukukhulupirira kuti. . .? Tsopano, kuyima pamaso pa munthu sikungakupangitse iwe kumverera chomwecho. Mukuona? Iwe ukudziwa kuti ndi chinachake pambali pa ine. Ndine basi ngati. . . Ngati desiki iyo pamenepo, iyo ndi desiki basi. Ndipo ine ndi munthu chabe. Koma iwe ukukhulupirira kuti uli mu Kukhalapo Kwake, osati kwanga; Kukhalapo Kwake? [Mlongoyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Zikomo. Mukuona? Iwe ukukhulupirira kwenikweni zimenezo, nawenso. Ndipo iwe ukuyenera kukhulupirira izo, chifukwa ine ndikuwona mthunzi, mwaona. Tsopano iwe ukuyenera kukhulupirira.

226 Tsopano iwe ukuvutika ndi mavuto amkati, ziwalo zamkati. Iwe unakhalapo ndi opareshoni. Uko nkulondola. Unapangidwa opareshoni, ndipo izo sizinathandize. Izo zikuvutitsabe. Uko nkulondola ndendende. Ndiye iwe umakhala ndi kupweteka kwa mutu kowirikiza apa kukukuvutitsa iwe. Tsopano iwe ukudziwa kuti chinachake chikuyenera kudziwa zinthu zimenezo, sichoncho izo? Iwe ukukhulupirira tsopano kuti ukhoza kuzilandira izo? Iwe ukukhulupirira izo? Chabwino, pita ukalandire izo ndiye, mu Dzina la Ambuye Yesu. Ameni.

Aliyense tsopano apemphere.

227 Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuwulula kwa ine chinthu chimene iwe ukuchikhumba? Kodi iwe ungakhulupirire zimenezo ndiye, kuti izo zingatero, mfundo imeneyo imene ili pa mbali yako ikhoza kuchokapo? Chabwino, ndiye kazipita ukakhulupirire izo, ndiyeno izo—izi zichita zimenezo.

228 Ndikudziwa kuti iwe wafooka. Ine sindikufuna kuti ndikusunge kuposa momwe ndingakuthandizire. Iwe ukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? [Mlongoyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Iwe ukutero. Ndine mlendo kwa iwe. ["Inde."] Ndipo ife sitikudziwana wina ndi mzake. Ngati ndingakhoze kukuthandiza iwe, ine ndithudi ndingachite zimenezo, dona. Ine ndingati—ndingayende, kukwawa, kukankha kotala ndi mphuno yangayi kudutsa m'misewu ya mzindawu, kuti ndikuthandize iwe, chifukwa ndiwe—ndiwe mwana, ndipo iwe waphimbidwa ndi mthunzi.

229 Ine ndikuzindikira tsopano, ine nditatha kuyankhula nawe ndi kunena zimenezo, iwe ukudziwa chimene chiri cholakwika. Kotero iwe ukudziwa kuti ukuyenera kufa nthawi yomweyo ngati chinachake sichichitidwa kwa iwe. Iwe uli ndi vuto la chikazi, izo ziri mu chikazi chako, ndipo icho ndi chotupa. Ndi khansa. Ndipo iwe ukuyenera kufa nthawi yomweyo ngati Mulungu sakuthandiza iwe. [Mlongoyo akuti, "Mwezi umodzi wowonjezera . . . ? . . . "—Mkonzi]. Uko nkulondola. Iwe ukukhulupirira kuti Iye akuchiza iwe? ["Inde, ine ndikutero."] Tawona, mlongo, icho ndi—icho ndi chiyembekezo chako chokhacho. Ukhulupirire izo pakali pano, ndi mtima wako wonse, ndipo ukhalire moyo Ufumu wa Mulungu.

230 Ine ndikusanjika manja anga pa dona wamng'onoyu, mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo ndikumutsutsa mdierekezi amene akutenga moyo wake. Mulole iye amusiye iye, ndipo mulole mtsikana uyu akhale moyo, chifukwa cha Ufumu. Ameni.

231 Mulungu akudalitse iwe, mlongo. Ukhulupirire izo tsopano ndi mtima wako wonse. Ukhulupirire ndi mtima wako wonse.

232 Wina, mthunzi. Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza izo ndi kupanga izo kukhala bwino, kuzichotsa izo kwa iwe? Unali ndi kumverera kwachirendo kwenikweni pamene

izo zimasamalidwa, sichoncho iwe? [Mlongoyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Izo kwenikweni, zinakusiya iwe apo pomwe. Uko nkulondola. Tsopano iwe ukhulupirire izo, ndi mtima wako wonse, ndipo izo zikhala kutali ndi iwe. Pita, ukukhulupirira. Mulungu akudalitse iwe. Chabwino.

233 Tayang'ana pa ine, mlongo. Kodi ukufuna kupita ukadye nkhomaliro yako ndi kukamverera bwino za izo kachiwiri? Basi kazipitirira. Chilonda cha mmimba chimenecho chikusiya iwe, ndipo iwe uchiritsidwa aponso. Chabwino.

234 Tayang'ana mbali iyi, dona. Iwe ukuwopa chiyani? Iwe uli ndi vuto la manjenje. Akhala akukuvutitsa iwe kwa nthawi yayitali. Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza manjenje amenewo ndi kukupanga . . . Nainte peresenti ya omvetsera awa akunjenjemera ndi chinthu chomwecho pakali pano. Ndipo uko nkulondola ndendende. Mukuona? Iwe umafuna malo oti uyikepo phazi lako nthawi zonse. Iwe, onse amakuuza iwe, "Uzilongosole wekha, ndipo ukhulupirire *ichi, icho.*" Koma iwe ukuyenera kukhala ndi malo oyambirapo. Iwe uli pa izo pakali pano. Ukhulupirire izo, iwe utero? Mawu a Mulungu akuti ndiwe mfulu. Iwe ukukhulupirira zimenezo? [Mlongoyo akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino, pita ndipo ukakhale womasuka ku chinthu chimenecho. Chabwino. Mulungu akudalitse iwe, mlongo.

235 Ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza matenda a shuga ndi kukupanga iwe kukhala bwino? [M'baleyo akuti, "Inde."] Ndipo iwe ukutero? Uzingopitiriza kumayenda, uziti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu. Ine ndipita ndipo ndikakhulupirira izo ndi mtima wanga wonse."

236 Manjenje, vuto lachikazi, ndipo iwe uli ndi vuto lachikazi. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza . . . Ndi vuto la mmimba, nalonso. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchiritsa iwe? Pita panjira yako, ukukondwera, ukuti, "Zikomo Inu, Ambuye."

237 Tayang'anani pa ine, bwana. Ndinu mwamuna wamphamvu wanyonga, koma mitsempha imeneyo ndi yofooka kwambiri. Inu mukukhulupirira kuti izo zithetsedwa usikuuno? Pitani, mukalandire izo mu Dzina la Ambuye Yesu. Mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Inde.

238 Bwera, mlongo. Tayang'ana mbali iyi. Inde, ine ndikukuwona iwe ukuyesetsa kudzuka, ndipo wolumala pambali ya bedi. Iwe uli ndi nyamakazi. Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiza iwe? Uzingopitirira, kukhulupirira izo, ndikuti, "Yesu Khristu wandichiritsa ine," ndipo ukhulupirire izo ndi mtima wako wonse.

239 Mlongo wanga, kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza matenda a shuga amenewo ndi kukupanga iwe

kukhala bwino, nawenso? Chabwino. Pita panjira yako, ukuti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu."

240 Bwera, dona. Iye akufuna kuti akupangitse iwe kukhulupirira kuti upenga misala. Iye wakhala akukuuza iwe zimenezo, koma iye ndi wabodza. Ndiwe mfulu tsopano. Pita kwanu ndipo ukakondwere, Yesu Khristu wakumasula iwe.

241 Ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza vuto la mmimba limenelo, ndikukupanga iwe kukhala bwino bwino? Kazipita panjira yako, ukusangalala, ukuti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu."

242 Bwera, dona. Tsopano chinthu chomwecho. Usawalole iwo kuti azikuuza iwe zimenezo. Ndi vuto la manjenje. Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiza iwe, usikuuno? Ndi chiyembekezo chako chokhacho choti uchite zimenezo. Yambapo panjira yako, ukusangalala, wokondwa, ndipo uzimwetulira, ndipo ukakhale monga momwe unkakhalira. Mukuona?

243 Inu mukukhulupirira ndi mitima yanu yonse? Ndi angati akukhulupirira tsopano ndi mitima yanu yonse, "Ine ndikukhulupirira"? Ine ndikukhulupirira kuti Yesu amapulumutsa, ndipo Magazi Ake amatsuka kuyeretsa kuposa chipale. Inu mukhulupirire zimenezo!

244 Nanga bwanji inu kunja uko mwa omvetsera, kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mupemphere tsopano, nenani, "Ambuye Yesu mwamunayo ali kutali ndi ine." Ena a inu kumbuyo kuno kwinakwake, chabwino, pempherani ndipo mukhulupirire zimenezo.

245 Bambo uyu wakhala kumbuyo komwe kuno, vuto la ndulu. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza nduluyo ndi kukupangani inu kukhala bwino? Inu, chabwino, chikhulupiriro chanu, inu munakhudza Chinachake. Ine sindikumudziwa iye, koma iye anakhudza Chinachake. Mukuona?

246 Dona uyo akusangalala, wapafupi ndi inu pamenepo. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa nyamakaziyo mwa iwe, dona, ndi kukupanga iwe kukhala bwino? Iwe ukukhulupirira zimenezo? Chabwino, iwe ukhoza kudzuka . . . Iwe ukhoza kukhala ndi ako.

247 Amene wakhala pafupi ndi iweyo, uli ndi vuto ndi diso lako. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu achiza vuto la diso limenelo ndi kukupanga iwe kukhala bwino? Chabwino, ngati iwe ukukhulupirira zimenezo, iwe ukhoza kukhala nazo izo, nawenso.

248 Wina wakhala pafupi ndi iwe, ali ndi vuto ndi mlomo. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa chophukacho pa mlomo wako ndi kukupanga iwe kukhala bwino? Iwe ukhoza kukhala ndi ako, nawenso.

249 Ine ndikukubetcherani inu kuti mukhulupirire zimenezo. Ameni. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu! Musakaikire. Mungokhulupirira! Mukhale ndi chikhulupiriro!

250 Dona wakhala apa, akuyang'ana kumbuyo uko moona mtima kwambiri, wakhala apo akuvutika ndi vuto la mtima. Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa vuto la mtima limenelo, ndi kukupanga iwe kukhala bwino, dona? Ngati iwe ukutero, ukhoza kulandira chimene ukuchipempha. Eya.

251 Tsopano iwe amene wayika mpango wako pa nkhope yako, iwe uli ndi vuto ndi khosi lako ndi nsana wako. Izo zinayambika chifukwa cha ngozi yagalimoto. Iwe unagundidwa mu galimoto, ndipo izo zinapweteka khosi lako ndi nsana. Kodi ukukhulupirira kuti ukhala bwino? Iwe ukhoza kulandira chimene wachipemphapo.

252 Nanga bwanji *muno*, winawake mkati muno akufuna kukhulupirira? Apo pakhala dona akuyang'ana pa ine, ndi wamanjenje kwenikweni, wakhala apo pomwe akuyang'ana pa ine. Uyo ndi mwana wake wamwamuna wakhala pafupi ndi iye, amene ali ndi vuto la mtima. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani awiri nonse a inu. Inu mukutero, kwezani mmwamba manja anu, nenani, "Ine ndikuzilandira zimenezo." Ndiye inu mukhoza kuchiritsidwa, mu Dzina la Yesu Khristu.

253 Makhalidwe a Mulungu amazidzindikiritsa Yekha. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali pano? Ndi angati muli okhulupirira? Ikani manja anu pa wina ndi mzake, pamenepo. Ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ikani manja anu pa wina ndi mzake, pamenepo.

254 Atate athu Akumwamba, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mdierekezi awasiye omvetsera awa, ndipo mulole iye akataidwe ku mdima wakunja.

64-0401 Khristu Wozindikiritsidwa Wa Mibadwo Yonse
4-H Club Barn
Louisville, Mississippi U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org